

CHIKOKA

 Zikomo inu, kwambiri. Tiyeni ife tikhale chiyimire kwa mphindi yokha tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa pemphero. Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndi mitima yathu, ndikudabwa ndi angati muno ali ndi chopempha, akhoza kupanga icho kudziwika kwa Mulungu pamene inu mukukweza manja anu? Ndiyeno tsopano ingogwirani chopempha chanu pamene ife tikupemphera.

² Atate Akumwamba, ife tiri okondwa kwambiri usikuuno chifukwa cha iyi, nthawi ina imene ife tingakhoze kubwera kwa Inu, ndi kukhala nacho chitsimikizo ichi kuti chimene ife tikupempha ife tilandira, ngati ife titi tikhulupirire kuti ife tilandira chimene ife tikuchipemphacho. Ndipo tsopano, Ambuye, thandizani kusakhulupirira kwathu, kuti ife tikhoze usikuuno kukhala okhoza kukhala nazo zinthu izi zimene ife tikuzipempha. Manja anga, ndi manja awo, ali mmwamba. Ndipo ife tikupemphera, Atate, kwa Inu Amene mukumvetsa zinthu zimene ife tikuzisowa. Perekani izi, izo, kwa ife, Ambuye, usikuuno. Ife tikupempherera chilimbikitso, kuti pamene ife tiri mu ora lalikulu ili la nsautso limene ife tirimo, ndi...ndipo dziko mu chikhalidwe chomwe ilo lirimo, ife tikusowa thandizo Lanu loyera kwambiri, Ambuye. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutilimbikitse ife ndi Mawu Anu, kuti ife tikhoze kudziwa momwe ife tiyenera kumachitira, kusanachitike kumene Kudza kwa Ambuye Yesu. Perekani izi, Atate. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Inu mukhoza kukhala pansii.

³ Wokondwa kwambiri kubwereranso usikuuno, ndi kudzayankhula kachiwiri za Ambuye wathu wachisomo kwambiri. Ndi zabwino kuti ndabweranso kuno mu Lane Tech kachiwiri. Izi ziri ngati kubwera kwathu; ine ndakhala pano nthawi zochulukana. Ndipo tsopano ine ndikuwona iwo ali nayo mipango yambiri pano yomwe yayikidwa pamwamba pano kuti ipemphereredwe. Ndipo tsopano, usiku wathawu, ife tinayenera kutero, ife tinatseka misonkhano yathu yachizolowezi ya machiritso, anatenga makadi athu ndi zinthu, chifukwa chokhala ndi misonkhano iwiri. Inu mwaona, izo zimakhala ngati zimaika kupsyinjika ndithu pa inu, pokhala ndi—misonkhano iwiri. Ndipo tsopano ife ndithudi tikhala tikupempherera mipango iyi usikuuno, ndi kudalira kuti Ambuye ampanga mmodzi aliyense wa inu, ndi chikhulupiriro kuti mudzalandire zomwe inu mwazipempha mu zopempha izi.

⁴ Ife ndithudi timusowa M'bale Mel Johnson mawa, ndi kuyimba kwabwino kumeneko. Ine ndikuyamikira kwenikweni

liwu labwino lija limene Ambuye anamupatsa iye.

⁵ Ndipo tsopano, mawa, ngati inu mukudzachezera kuno, ine ndidzanena kwa anthu aku kachisi, pali... Ine ndiri nawo abwenzi ena kuno ochokera uko ku Jeffersonville. Ine ndikuganiza ku mpingo wa Philadelphia, M'bale Mead, m'bale wathu, ine ndikuganiza iwo ali ndi utumiki kumeneko. Ndipo ine sindikudziwa ngati inu, inu muli ndi msonkhano? Ulipo msonkhano. Inu, nthawi yanji? [M'bale akuti, "Leveni."—Mkonzi]. Leveni koloko, kudzakhala kuli msonkhano kumeneko. Ndipo ine ndikuganiza ine ndidzabwerera pafupifupi hafu pasiti wani, kapena thuu, zina... Firii, ine—ndidzayenera kudzakhala pa firii, firii koloko, ndipo—ndiyeno seveni kenanso mawa usiku. Kotero ife ndithudi tikufuna kukuitanani mwachikondi nonse inu kuti mubwere ku misonkhano, ngati inu mulibe msonkhano ku mpingo wanu womwe.

⁶ Ife ndithudi sitingafune kukuchotsani inu pa malo anu omwe antchito, chifukwa icho si cholinga chathu. Ndiko kuyesera kugwira, makamaka, iwo amene sanapulumutsidwe. Iwo amene alibe Mzimu Woyera, ndipo inu—inukhulupirira kwenikweni kuti inu mukuwusowa Iwo, ndiyeno ife tiri pano kuti tikuthandizeni inu. Ndiye odwala ndi osautsika, bwanji, ife tiri pano kuti tiwapempherere iwo, kuchokera mmpingo yonse. Ndipo mubwerere ku mpingo wanu, kulikonse kumene inu mukuchokerako. Ngati mwalandira Mzimu Woyera, kapena mwachiritsidwa, bwererani ndi umboni, mukawauze enawo. Ngakhale ngati mpingo wanu sumakhulupirira mu zimenezo, mupitebe mulimonse. Mukuona? Kumene, ndi zophweka kulola Kuwala kwanu kuziwala pamene pali kochuluka kwa—kwa Kuwalako, koma ife tikufuna Kuwala kuwalire kumene kulibeko Kuwala. Ndi pamene iko kumapereka chikoka chake chabwino kwambiri.

⁷ Ndipo... (Zikomo inu, M'bale Vayle.) [M'bale Vayle akusintha maikrofoni, ndikuti, "Mukhale mmwamba monga *chonchi*, ife tiyenera kuti tiziwone izo."—Mkonzi]. M'bale Vayle amaganiza kuti iwo amalephera kuti amve. Kodi ziri bwino? Chabwino, chabwino, zimenezo ziri zabwino.

⁸ Tsopano, usikuuno, popanda msonkhano wa machiritso, ine ndikuganiza, ine ndiyenera kutulukamo mofulumira pang'ono usikuuno. Ine—ine ndakhala ndikunena, usiku uliwonse, "Ine ndiyesetsa kuti ndikutulutseni inu pafupifupi hafu pasiti-naini." Ndipo pafupifupi kwambiri nthawi imeneyo tsopano, ndipo kotero, naini koloko, pafupifupi maminiti faivi ake. Ndiyeno nthawi yomwe ine nditi nditsirize, ndiyeno ndikukusungani inu mmawa uno pafupifupi maora awiri, ine ndikuuzani inu, inu mwinamwake mudzakhala otopa ndi kumasangalala pamene ine ndizidzanyamuka mu mzinda mawa usiku. Koma ine ndikukhumba ine ndikanangodzibweretsa ndekha ku zokambirana za maminiti twente zimenezo. Koma

ine ndimangoyenera kumangoyankhula mpaka ine nditatopa, ndipo ine ndikudziwa inu mumakhala mwatopa pofika nthawi imeneyo. Kotero ndiye ine sindimatsiriza basi; ine ndimangosiya ndi kulowa mkati, kukapumulira pang'ono.

⁹ Tsopano, usikuuno, ine ndikufuna inu mutembenezire mu Mabaibulo anu, ku Yesaya, Bukhu la Yesaya mu—mutu wa 6 wa Yesaya. Ndipo tsopano ife tisanawerenge, ife tingamufunse Mulungu kuti adalitse Mawu Ake ndi ku—kuwapanga Iwo enieni kwa ife, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu mphindi yokha. Chabwino, ife tiwerenga Mawu poyamba, ndiyeno mvetserani mwacheru tsopano pamene ife tikuwerenga.

Mchaka chimene mfumu Uziya anamwalira ine ndinali...ine ndinawonanso Ambuye atakhala pa mpando wachifumu, pamwamba ndipo anakwezedwa pamwamba, ndipo ulemelero wake unadzaza mkachisi.

Ndipo pamwamba pake panadzayima aserafi: aliyense anali ndi mapiko sikisi; ndi awiri iye anaphimba nkhope yake, ndipo ndi awiri iye anaphimba mapazi ake, ndi awiri iye anaulukira.

Ndipo wina anafuulira kwa mzake, ndipo anati, Woyera, woyera, woyera, ndi AMBUYE Mulungu wa makamu: dziko lonse ladzaza ndi ulemelero wake.

Ndipo mphuthu za chitseko zinasuntha pa liwu la iye amene anafuula, ndipo nyumbayo inadzazidwa ndi utsi.

Ndiye ine ndinati, Watsoka ndi ine! pakuti ine ndathedwa; chifukwa ndine munthu wa milomo yonyansa, ndipo ine ndimakhala pakati pa anthu a milomo yonyansa: pakuti maso anga awona Mfumu, AMBUYE wa makamu.

Kenako mmodzi wa aserafi anadzawulukira kwa ine, ali ndi khala lamoto mu dzanja lake, limene iye analitenga ndi zopanira kuchokera pa guwa:

Ndipo iye analiyika ilo pakamwa panga, ndipo anati, Taona, ili lakhudza milomo yako: ndipo mphulupulu zako zachotsedwapo, ndipo tchimo lako layeretsedwa.

Ndiponso ine ndinamva liwu la Ambuye, likuti, Ndani yemwe Ine nditi ndimutume, ndipo ndi ndani adzatipitire ife? Ndiye ine ndinati, Ndine pano; nditumeni ine.

¹⁰ Tiyeni ife tipemphere. Ambuye Yesu, ife sitiri okwanira kuti tilowe m'mutu wachisomo kwambiri uwu, usikuuno, koma ife tikupempha thandizo Lanu tsopano, Ambuye, pakuti palibe cholinga china koma kuti—Uthenga ukhoze kulalikidwanso mu mzinda wa Chicago. Perekani izi, Ambuye. Ndipo mulole chi—chikoka chikhale chikoka chosatha. Perekani izi. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹¹ Tsopano ine ndikufuna kuti nditenge mutu kuchokera pa awa, wa: *Chikoka*. Inu mukudziwa, pali chinachake china chimzake chimene ife tiri, ife, zimene ife timachita, ife timakopa winawakenso ndi zimene ife timachita, momwe ife timachitira, momwe ife timayankhulira, momwe ife timakhalira. Ndipo zonse zomwe ife timachita, ife timamukopa winawakenso.

¹² Ndipo tsopano, inu mukudziwa, anthu ambiri samapita ku tchalitchi. Iwo amati... Chabwino, iwo ali ndi malingaliro olakwika a tchalitchi. Iwo amaganiza kuti ndi a—akazi kumusi uko ndi—ndi afiti, ndipo a—amuna ali—ali ndi ziwanda zovala zakuda, ndipo iwo anangokhala ndi lingaliro lolakwika pa izo. Koma ine ndikuuzani inu zimene iwo amachita, iwo amayang’ana moyo wanu kuti awone zomwe inu mumachita. Ine ndikukhulupirira anali Paulo yemwe anati, “Ndife akalata olembedwa a Mulungu, owerengedwa ndi anthu onse.” Pamene inu muli pa msewu, ndipo pamene inu muli kuntchito kwanu, ndipo kulikonse komwe inu muli, winawake akukuyang’anani inu.

¹³ Ndipo makamaka mutatha kunena ndipo mwapanga kuvomereza kwanu kuti ndinu Mkhristu, iwo adzakuyang’anitsitsani inu moyandikira kwambiri pamenepo, ndipo izi zimapereka chikoka kwa—kwa anthu omwe ali pafupi nanu. Ndipo ife tiyenera kumasamala zimene tikuchita. Chifukwa, ngati tikupereka chikoka cholakwika, ndiye kuti tikubweretsa chitonzo, osati kwambiri pa ifeeni, koma pa chimene ife timadzinenera kukhala: Akhristu. Ife timachibweretsa icho pa Khristu. Ndipo palibe mmodzi, ngati ife tingaganize, inu simungafune kubweretsa chitonzo pa Khristu. Koma mchitidwe wolakwika, pa nthawi yolakwika, udzayambitsa kulingalira kolakwika kwa munthu amene akukuyang’anani inu. Ndipo aliyense amayang’anidwa, pamene iwe ukudzinenera kuti ndiwe Mkhristu.

¹⁴ Tsopano ndime iyi yomwe tikuyankhulapo usikuuno, ya chikoka, iyo ikubwerera, phunziro lenileni la izo, ngati inu mukufuna kuti—kuti muwerenge izo, inu mulipeza ilo mu Mbiri Yachiwiri, mutu wa 26. Unali moyo wa Uziya uyu, mfumu.

¹⁵ Tsopano, Uziya mfumu anali mnyamata woweta. Iye anali mnyamata wamng’ono, yemwe, mwana wa mfumu, ndipo amene anakonda zomatuluka kunja. Iye—iye anakonda—nkhalango ndipo iye anali wolishya ng’ombe. Iye anakondanso minda ya mpesa, iye anakonda kukawona zinthu zikumera. Ndipo mnyamata wamng’ono uyu analeredwa pansu pa chikoka chabwino kwenikweni. Amaziya, bambo ake, anali munthu wamkulu, mmasiku ake otsiriza iye analekerera pang’ono, ndipo anatola milungu inayo kuchokera ku dziko lina, ndipo Ambuye ndiye anamuchotsa iye pa dziko lapansi. Koma mnyamata uyu anali nako kukopa kwabwino, chifukwa amayi ake anali mwana

wamkazi wa Yerusalemu, abambo ake wokhulupirira, ndipo chotero a—mnyamatayo anali ataleredwa ndi chikoka chabwino.

¹⁶ Ndipo ndiyo njira yabwino yolerera mwana, mu njira yomwe iye azikhalira. Ndipo inu mukudziwa chiyani? Ana anu ndi amodzi a maso aakulu amene amakuyang'anani inu. Iwo amayang'ana zomwe inu mukuchita. Ndipo chirichonse chimene inu muchita, iwo amakutsanzirani inu, chifukwa inu mukuyika chitsanzo pamaso pa iwo, pa zimene inu mukuchita.

¹⁷ Zikundikumbutsa ine. Kuno osati kale kwambiri, ine ndinali pa msonkhano wa Full Gospel Business Men, uko mu Los Angeles. Ndipo M'bale Oral Roberts anali atapanga neno la chinachake pa mzere uwu, ndipo iwo anandifunsa ine kuti ndidzuke ndi kukanena chinachake pa izo, za kukopa. Ine ndinati:

¹⁸ Izo zikundikumbutsa ine za nkhani yomwe ine ndinawerengapo kamodzi, kumene a—bambo anatuluka, Usiku wa Khristimasi, amatenga mphatso kumadutsa nazo mwa oyandikana, kwa azimzake, oyandikana nawo. Ndipo nthawi iliyonse, kumene iye wapita ku malo, iye—iye amakamwa chakumwa. Iye amapita ku nyumba yotsatira, ndipo iye amakhoza kukatenga chakumwa. Ndipo pa nthawi imene iye wamalizitsa zake zonsezo—kupereka mphatso zakezo, ndi zomwe iye anali atazisonkhanitsa, panjira pobwerera iye anaganiza kuti atenge njira yachidule kudutsa pa parki. Ndipo kunali kutagwa pafupifupi mainchesi foro kapena sikisi a chisanu. Ndipo iye anadzipeza yekha, iye sakanakhoza kuyenda molunjika, iye anali kuyenda mokhotakhota chifukwa iye anali atatengeka ndi zakumwa izi.

¹⁹ Iye anazindikira, akubwera mmbuyo mwake kutali, samakhoza kumayenda pafupi ndi iye, anali mnyamata wake wamng'ono, mnyamata wamng'ono wa zaka seveni zakubadwa; ndipo iye anali akupanga masitepe aakulu, ndi kumagwa, ndi kumakhotakhota. Kotero iye anadikirira mpaka mnyamata wamng'onoyo anamupeza iye, ndipo iye anati, “Kodi iwe ukuyenderanji choncho, mwana wanga?”

Iye anati, “Adadi, ine ndikuyesera kuti ndiziponda mmasitepe anu.”

²⁰ Tsopano inu mukuwona kuti izo ndi zoposa chabe—chitsanzo, chifukwa icho ndi choonadi, kuti, ana anu, inu mumayika mayendedwe kwa iwo.

²¹ Ndipo ngati anthu athu Achimereka akuika mayendedwe lero, pamaso pa ana athu, za kusuta ndudu, akazi ndi amuna, kumwa, ndi makadi mnyumba, ndi—ndi daisi, ndi mtundu wanji wa—wa anthu omwe ife tidzakhale nawo mu mtundu wotsatira umene uli nkudza, kapena m'badwo wotsatira, kani, umene uli nkudza? Ilo lidzakhala gulu la amisala. Ndipo chimene ine ndikuganiza kuti dziko lonse liri basi pafupifupi

mu chikhalidwe chimenecho tsopano. Ndiye ngati mtundu uwu, kapena m'badwo uno, kani, uli monga chonchi, kodi wotsatirawo udzabala chiyani? Ndiye ngati pakanati padzakhale wina, bwanji, mtundu wonse wa anthu, ngati iwo ungamapitirire momwe iwo ukuchitiramu, udzatheratu, limodzi, chifukwa ife tikudzipha tokha ndikupereka zitsanzo kwa ena.

²² Ndipo ngakhale Akhristu lero, amene amadzinenera kuti ndi Akhristu, ndi kumasuta ndi kumamwa, ndi—ndi kunama, ndikupezeka wosakhulupirika. Pamene ife... Bwanji, izo sizodabwitsa kuti Chikhristu chiri pa amodzi a malo ake ofooka pa nthawi ino. Ndiko kukopa komwe anthu a mpingo ali nako—ayika pa amuna amene sanalandirebe Khristu. Amuna akufuna kusunga umboni wawo ndiyeno nkumakhala mulimonse momwe iwo akufunira.

²³ Koma ndicho chifukwa chake Mzimu Woyera uli *chokakamiza*—chotsimikizika mu tsiku lino, chifukwa Iwo ndi Umodzi umene umakhala moyo wanu. Inu simumaukhala iwo inueni. Ndi Khristu mwa inu, ndiye, inu mutatha kulandira Mzimu Woyera. Ndipo, ndipo ngati Iye alibe uyambiriro mmoyo mwanu, ndiye inu musingokumbukira, inu simunalandire Mzimu Woyera. Chifukwa, ngati Iye ali mwa inu, Iye adzakhala Moyo Wake Womwe. Inu simulinso mwa inu eni. “Inu ndinu akufa, ndipo moyo wanu wabisika mwa Mulungu, kudzera mwa Khristu, ndipo mwasindikizidwa ndi Mzimu Woyera.” Kotero palibe njira nkomwe kuti inu mukhalenso inueni nkomwe, chimene inu munali.

²⁴ Tsopano, mnyamata wamng'ono uyu, ife tikupeza kuti, iye, pokhala ndi kholo labwino ili, laumulungu ndi kuphunzitsidwa, izo... Pamene abambo ake anamwalira, pamene iye anali ndi zaka sikisitini zokha zakubadwa, ndipo anthu anamutenga ndi kumupanga iye mfumu. Ndipo iye anadzabwera pa mpandowachifumu wa mphamvu pamene iye anali usinkhu wa zaka sikisitini zokha. Ndipo ngati inu mungawerenge moyo wake, iye sanakopedwe ndi ndale za dziko lake. Iye—iye sanatenge ganizo lotchuka. “Iye ankafunafuna Mulungu,” Baibulo linatero.

²⁵ Tsopano, ndicho, icho chinali chimene chinamupanga iye chitsanzo chachikulu chotero kwa mneneri wamng'ono uyu, pa nthawi yomweyo, Yesaya. Mneneri Yesaya anakhala moyo mmasiku a mfumu Uziya. Ndipo awiri onsewo pokhala aang'ono limodzi, mneneri ndi mfumu, iwo anali abwenzi opambana limodzi. Ndipo Yesaya ankakhala ku nyumba ya chifumu, ndipo iye ankatsamira pa nkono wa—wa mfumu. Ndipo ife tikupeza kuti chikoka cha mnyamata uyu chinamukoka Yesaya. Iye anadzakhala ngwazi kwa—kwa Yesaya, chifukwa (iye anali) iye sanapange kusintha kulikonse mwa anthu, iye sanalole chirichonse chimuchotse iye kuchokera ku mbali imodzi kupita ku imzake. Iye anatsimikiza kuti azimutumikira Mulungu,

ndi kutumikira Mulungu yekha. Ndipo ameneyo ndi munthu wabwino kutengerapo chitsanzo. A. . .

²⁶ Ndipo ife tikupeza kuti iye sananyengerera konse ndi lirilonse la maiko achikunja, dziko lachikunja; iwo atamuwona iye akumanga ufumu wake waukulu kwambiri, ndipo Mulungu anali ndi iye ndipo amamudalitsa iye.

²⁷ Ndipo Mulungu adzamudalitsa munthu aliyense amene ati adzakhale ndi Mawu Ake. Tsopano, ndizo, Mulungu amakhala wokakamizika kuchita zimenezo, kuti amudalitse munthu aliyense amene angakhale ndi Mawu a Mulungu.

Tsopano ife tikuwona kuti Yesaya anaikondadi mfumu imeneyi.

²⁸ Ndiyenyo ufumu wa mfumu unafalikira. Ine ndikuganiza iye anali pafupi ndi Solomoni, mu ufumu wake, chifukwa chikoka chake chinafikira mtunda wonse mpaka ku Igupto.

²⁹ Ichu chinali thandizo lalikulu kwa Yesaya, mneneri wamng'ono, kuwona kuti munthu aliyense amene angaime ndi Mulungu, ndipo mosalabadira za ndale kapena china chirichonse, iye amakhala molunjika ndi Mawu. Iye ndithudi anali chikoka kwa mneneri, Yesaya. Mnyamata uyu, momwe Mulungu anamudalitsira iye, chifukwa iye anakhala moona ku Mawu.

³⁰ Tsopano ife tikupeza kuti mfumu iyi, oh, inachita monga Akhristu ambiri a lero. Bola ngati iye amakhala wodzichepetsa, ndiye Mulungu amamudalitsa iye. Koma Baibulo linanena apa, kuti, “Pamene iye anakwezedwa mmwamba.” Pamene anadzapeza kuti chirichonse chikumutetezera, ndiye iye anadzadzikweza mwa iyemwini, ndipo zitatero iye anali pa njira yake yotulukira.

³¹ Tsopano, izo ziri chomwecho, izo ziri lero, ndi—ndi mipingo. Izo nthawizonse zakhala ziripo, kuti pamene anthu amverera kuti iwo akhala okwanira, iwo sakusowa kuti azipempheranso, iwo sakusowa kuti azidikirira pa Mulungu kwa utumiki wawo.

³² Ngati mungandikhululukire kalankhulidwe aka, ine ndikugwirizana ndi wolemba winawake, kuti ndi zomwe zapangitsa ambiri a amuna awa omwe akhala ali mu zitsitsimutso za masiku otsiriza ano, kapena chitsitsimutso cha tsiku lotsiriza ichi, kuti—kuti awuluke mzidutswa. Ena a iwo anapezeka kuti iwo ankanenedwa kuti anali ataledzera paguwa lawo, ndipo—ndipo ena a iwo achita zolakwika. Ndi chifukwa chakuti iwo—iwo ali ndi chikoka choterocho pa anthu mpaka iwo amayamba kumverera kuti ndi odzidalira pawokha, kuti umenewo ndi ufumu wawo wawung'ono, ndipo iwo akhoza, iwo awagwira anthu mmanja mwawo kwambiri mwakuti iwo akhoza kumangochita chirichonse chimene iwo akufuna kuchita, ndipo anthu sakuzindikira izo. Koma Mulungu amazindikira izo, inu mukuona, ndi Mmodzi ameneyo.

Ine ndikhoza kunena kuti...Monga Nebukadinezara, tsiku lina, anatuluka ndipo anati, “Taonani ufumu waukulu chotani umene ine ndamanga,” ndipo kenako Mngelo wa Ambuye anamukantha iye.

³³ Ndipo pamene mwamuna kapena mkazi, ziribe kanthu kaya iye ndi bishopu kapena kardinalo, kapena chirichonse chimene iye angakhale ali, pamene iwe uyamba kudzimva kuti ndiwe wodzidalira wekha, ndiye kulibwino uyambe kuyang’anitsitsa ndi kumasamala. Chifukwa, Mulungu sadzakulola iwe kuti uzipita monga chomwecho, chifukwa Iye sagawana ulemelero Wake ndi aliyense. Ayi, bwana. Mulungu amadzitengera ulemelero, yekha.

³⁴ Nthawizina Mulungu akhoza kumudalitsa munthu ndi kumupatsa iye utumiki wawung’ono wabwinoko pang’ono kuposa abale ake, kapena osati wabwinoko, koma basi chinachake chosiyana pang’ono ndi abale akewo. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, munthuyo amadzikweza, ndi chidali chake atachitulutsa, ndipo, oh, mai, iye amakhoza, iye akhoza kukukankha iwe pa msewu. Ndipo, iyo, ndiyo nthawi yomwe ine ndikukhulupirira kuti munthu ameneyo wayamba kutuluka panja pa khomo, chifukwa Mulungu sangakhoze kumugwiritsa ntchito munthu wonga ameneyo.

³⁵ Mfumu iyi, ngakhale pokhala munthu waumulungu monga iye anali, iye anadzimva kuti ndi wokwanira payekha. Iye anadzimva kuti iye akhoza kudzikweza iyeyekha monyada, kuti iye akanakhoza kungotenga ulamuliro ndi kumachita chirichonse chimene iye ankafuna, palibe wina aliyense yemwe iye akanati amufunse.

Koma, kumbukirani, ife nthawizonse timakhala pansu pa Mulungu. Mulungu ndiye Mulungu wathu.

³⁶ Ndipo ife tikupeza kuti, iye anadzikweza mmwamba, ndipo iye—iye anadzikweza mmwamba kwambiri mpaka iye anaganiza kuti, chifukwa iye anali ‘atadalitsidwa ndi Mulungu,’ iye akanakhoza ‘kutenga malo a mtumiki,’ kotero iye anatenga zofukizira ndipo analowa mkati kuti akatenge malo a mtumiki. Iye anachoka pa malo a ntchito yake.

³⁷ Ndizo zomwe nthawizonse ndakhala ndikunena kwa Amuna Amalonda a Full Gospel awa, “Musadzayesere konse kukhala alaliki.” Alaliki amakhala ndi nthawi yovuta mokwanira kuti chinthucho chizikhala chowongoka. Ndiyeno ife tikuchita ntchito yosauka kwambiri kuchokera mwa iyo ndiyeno makamaka kumutenga mwamuma wamalonda amene sanayitanidwe nkomwe ku ntchitoyo. Mwaona, pamene inu muchita zimenezo, inu mukudutsa malire anu.

³⁸ Ndipo inu mukhoza kutenga phunziro pa izi. Kuli anthu ambiri kunja uko, ngakhale pa guwa usikuuno, akulalikira, amene sakuyenera kukhala pamenepo, chifukwa zangokhala

mochuluka tikiti yodyera, kapena kuti akhale otchuka pakati pa anthu, kapena—kapena kuti akhale ndi a—a—zochuluka pang’ono kuposa zimene winawake ali nazo, kapena kutamandidwa pang’ono ndi winawake akamakusisita iwe pa nsana, kapena chinachake. Mwaona, nthawizina iwo amadzakhala wansembe.

³⁹ Yesu anati, “Inu mumawononga nyumba za akazi amasiye, ndipo mumalalakala mipando yaulemu, ndipo, kuti mungodziwonetsera, mumapanga mapemphero aatali.” Iye anati, “Inu mudzangolandira chilango chochuluka choterocho chifukwa cha izo.” Mukuona?

⁴⁰ Ife—ifetse tisamatero, konse, kufika pamalo amenewo. Ife nthawizonse tizikumbukira kuti Mulungu amafuna kuti ife tikhale odzichepetsa. Njira yopitira mmwamba ndi pansi. Dzichepetseni nokha, ndipo inu mudzakwezedwa. Ndipo ngati inu mudzikweza nokha, inu mudzatsitsidwa pansi.

⁴¹ Tsopano ife tikupeza kuti munthu uyu anayesetsa kuti atenge malo a mtumiki, chimene iye sanali woyenera.

⁴² Komabe, Mulungu anamudalitsa iye, iye anali munthu wopambana. Iye analimbikitsa ufumu wake polimbana ndi mafuko onse a padziko lapansi. Iwo anali kubweretsa ulemelero ndi kumapereka izo kwa iye, nkhusa ndi ng’ombe. Ndipo iye anali ndi azibusa, ndi mpesa—okonza minda ya mpesa ndi, oh, chirichonse. Iye amakhala moyo wawofuwofu, kenako anayamba kumadzitukumula.

⁴³ Ife tikupeza kuti ngakhale mpingo, mpingo wamba ukhoza kukhala wodzichepetsa ndi kukhala ndi a—malo aang’ono nkumatumikira Ambuye ndi kuwona kwa mtima; ndipo mungowasiya iwo akhale ndi abwinoko pang’ono, winawake wawathandizira iwo ndipo apeza a—tchalitchi chabwino, kapena iwo adzayesera kuchipanga icho kukhala chabwinoko pang’ono kuposa china chimene chiri uko pangodya, ndipo kenako osonkhanawo amayenda ndi chidali chawo panja. Chimenecho, mwaona, ife—ifetse tiyenera tizikumbukira, chimenecho ndi chinthu cholakwika.

⁴⁴ Mulungu anauza Israeli, “Pamene iwe unali, Ine ndinakupeza iwe kuthengo, iwe unali wamagazi,” ndipo chikhaliidwe chimene iwo analimo, “ndiyeno pamene zinakukwana, ndipo—ndipo unadzikongoletsa, ndiye izo...” iye anatembenuzira nsana wake kuchoka kwa Mulungu, ndipo ana-... anasewera gawo la—la wachiwerewere, ndipo anayitana aliyense kuti adzamuwone iye. Ndipo ife tikuwona kuti Mulungu samakondweretsedwa nazo konse zimenezo.

⁴⁵ Ndipo ngakhale mfumu yayikulu iyi, yamphamvu ya Israeli apa, pamene iye anayesera kuti adzipange yekha kutenga malo amene iye samayenera kutero... sanadzodzedwe kutero. Ndipo ife tikupeza kuti—ansembe apa, anathamangira mmenemo ndipo

anakamuuzi iye, “Amenewo si malo anu. Inu simukuyenera kuti muzichita zimenezo, pakuti Mulungu wawapatulira amuna ku izi.”

⁴⁶ Oh, ngati utumiki ukanangokwanitsa kokha kufika pa malo amenewo, opatulidwira ku utumiki! Ngati anthu akanakhoza kuzindikira kuti kulalikira Uthenga si kupeza mamembala ambiri mu mpingo, koma ndi kudzipereka ku—cholinga cha ntchitoyo, kuti ife tiyenera kukhala ndi makanda obadwa kumene mu Ufumu wa Mulungu. Ziribe kanthu chipembedzo chimene iwo akupitako, kapena bwanji za izo, ndi kungopeza makanda obadwa kumene amenewo.

⁴⁷ Ndiye ife tikupeza kuti lero zimakhala zovuta kwambiri pamene timuwona mtumiki akuwuka ndi pang’ono, mtundu wina wa chodabwitsa chimene Mulungu waika mu utumiki wake. Ife timapeza kusanzira kwa chithupithupi kwa izo, kuti osiyanasiyana amabweramo ndi kudzayesa ku—kudzanena kuti *izi* ndi, iwo ali ndi *izi*, kapena amachita chinachake mosiyana pang’ono.

⁴⁸ Ine ndikudziwa za munthu mdziko lero, munthu wabwino, nayenso, munthu wabwino, mlaliki weniweni wa Mawu, ndipo ine—ine ndinganene kuti a—m’bale weniweni, ndipo ine ndinayankhula naye iye osati kale kwambiri. Ndipo iye ankakhala ndi zogirigisha, ndipo iye anamanga utumiki wake kwathunthu pa zogirigisha, tsopano iwo akumabatizira ku Moyo Wamuyaya, “anthu sikuti adzafa.” Ine ndikuwopa iwo ali kunja pa nthambi mwakuti iwo sadzakhala nayo konse njira yobwerera ku zimenezo, mwaona, koma chifukwa izo ndi zolakwika.

⁴⁹ “Munthu amene wabadwa mwa mkazi ali ndi masiku owerengeka, ndipo wodzadza ndi zisoni, zowawa.” Ndipo amoyo amadziwa kuti iwo ayenera adzafe. Ndipo ife tikudziwa, “Kunayikidwa kamodzi kwa munthu kuti afe, ndipo pambuyo pake chiweruzo.” Koteri, ife tikudziwa kuti tiyenera tidzatero.

⁵⁰ Ine sindikufuna kukhala mnyumba yakale ya tizirombo iyi imene ndikukhalamo. Iyo imagwidwa ndi matenda aliwonse omwe amayandamamo. Ine ndikufuna ina yomwe sinapangidwe ndi manja, yopangidwa motengera Mulungu, imeneyo—imeneyo si chomera cha haibridi monga iyi. Ine ndikufuna imodzi yomwe inapangidwa ndi manja a Mulungu, yomwe nthenda ndi matenda ndi imfa zimachokako kwa iyo. Tsopano, nthawi iliyonse Iye adzandiyitana ine, ine—ine ndidzakhala wokonzeka, mwa chisomo cha Mulungu, kukhulupirira kuti, “Pamene msasa uwu wapadziko lapansi udzapasuka, ife tiri nawo kale umodzi ukuti yembekezera,” limene tidzalowamo, limene sitingakhosenso kudza mwa ilo.

⁵¹ Kodi inu mungafunirenji kudzakhala mwa ili? Osati ine. Ndi wanga. . . Ife tikutuluka mwa ilo, ndipo ndine wokondwera

nazo izo. Ndipo munthu wakale uyu, msampha wa majeremusi womwe ife tikukhalamo, msampha wa imfa ndi zina, ndi kubuula ndi zowawa mmenemo, ndi ukalamba, ndipo bwanji, mai, ndani angafune kukhala mu thupi ngati limenelo? Ine, ndine wokondwa kuti pali limodzi limene likubwera. Ife tiri nalo thupi lomwe—lomwe likukonzedwera ife, mu Ulemelero. Ndipo mwamsanga pamene moyo udzachoka mthupi lakale ili pano, Mzimu Wamuyaya uwo wa Mulungu umene ukukhala mkatimo, udzatenga ulendo wake kupita ku kachisi uyo kutaliko, ndipo kumeneko iwo ukakhala Kwamuyaya. Ndi chifukwa chiyani kuti ife tifune chinachake ngati ichi? Mai! Inde, bwana. Oh, ine—ndine wokondwa kwambiri kuti, kuti apo, kuti alipo Mulungu Amene wazipanga zinthu zonse izi kukhala zomveka.

⁵² Ndipo ife tikuyang'ana apa, ife tikuwona iwo ndi mthunzi chabe, mulimonse. Ife ndi mthunzi. Ine ndikuyang'ana apa pa nsanja, ndikuwona amuna amene akuyenda, ndipo ine ndimayang'ana kunja pa msewu ndipo ndimawona amuna ndi akazi omwe akuyenda. Iwo ali nawo moyo, komabe iwo sungakhoze kukhala Moyo weniweni, chifukwa muli imfa mmenemo. Ndipo—ndipo Davide anati, “Ine ndidzayenda kudutsa mu chigwa cha mthunzi wa imfa.” Tsopano, izo zimatengera kuwala kochuluka kuti papangike mthunzi. Payenera kukhala kuwala kochuluka. Ngati ponsepo pali mdima, iwo sungakhoze kupanga mthunzi. Mukuona? Iwo uyenera kukhala kuwala kochuluka chomwechi, mumdima, kuti upange iwo kukhala mthunzi. Chabwino, tsopano izo zimatengera mbali iti mwa mbali imeneyo imene iwe ukutsamirako.

⁵³ Ngati ndimuwona mwamuna akuyenda, mwamuna wachichepere wowoneka bwino, mu zaka pang'ono, kudzawona tsitsi lake lachita imvi ndipo likuthothoka, mapewa ake akugwera pansi. Mtsikana wamng'ono wokongola atayima, ali ndi nkhope yoyera, yaumulungu pa iye, ndipo waimirira ndi kumatamanda Mulungu, ndipo ndikamadzabwerera mzaka pang'ono ndi kumupeza iye ali ndi mapewa-akugwa, atanyamula ana awiri kapena atatu. Chabwino, mai, pamenepo, izo zikusonyeza kuti mu thupi limenelo muli imfa. Ziribe kanthu momwe ilo liriri labwino ndi momwe likuwonekera lokondedwa, ilo likadali ndi imfa mwa ilo.

⁵⁴ Tsopano ine ndimayang'ana mbali yomwe mzimu umenewo ukutsamira mmenemo. Ngati iwo nthawizonse ukuyimira Kuwala, kuyankhula za Kuwala, kuyankhula za Kuwala, iwo udzapita ndi Kuwala. Koma ngati iwo nthawizonse umakhala kumbali inayo, ya dziko, zinthu za mdziko, kukopedwa ndi dziko, palibe china koma iwo udzatembenukira ku mdima pamene iwo udzafa, kukalowa mu mdima wakunja. Koteri inu mukuona, chimene ife tiri, ife tiyenera kukumbukira kuti ife tiri kokha chimene ife tiri mwa chisomo cha Mulungu, ndipo

palibe aliyense wa ife angakhoze kudziabwekerera za zimenezo. Ife tikhoza kungogwada mu kupembedza ndi kudzichepetsa, pamaso pa Mulungu, ndi kupereka matamando kwa Iye chifukwa cha ubwino Wake.

⁵⁵ Ndipo ife tikupeza kuti utali wonse pamene mfumu iyi inkamverera mwanjira imeneyo, Mulungu ankamudalitsa iye. Koma pamene iye anadzafika pa malo amene sanafune kukhala mu maitanidwe ake a iye mwini, iye ankafuna kuti atenge kuyitana kwa chinachakenso. Ndipo iye anaganiza, chifukwa chakuti Mulungu anali atamudalitsa iye, kuti izo zinali zabwino, iye akanakhoza kuchita zimenezo.

⁵⁶ Koma ndi momvetsa chisoni bwanji momwe ife timapangira kulakwitsa kumeneko! Motani, zoyipa bwanji! Iwe, iwe uyenera mwamtheradi uzikhala woonamtima. Iweu sumayenera, iwe usamachite kalikonse kupatula Mulungu atakulozera kwa izo, ndi kuzitsimikizira izo, ndi kuzivomereza izo, ndipo iwe nkudziwa kuti ndi Mulungu amene akuchita zimenezo.

⁵⁷ Kawirikawiri, munthu wa Mulungu, Mulungu amayenera kumutsitsa iye ndi kugwira munthu weniweniyo wa Mulungu. Si anthu amenewo amene amafuna zinthu zambiri kuti achite zambiri nazo izo, iwe ungavutike kudziwa zomwe iwo angachite nazo izo ngati iwo atazilandira izo. Mukuona? Koma Mulungu kawirikawiri amayenera kumugwira munthu Wake, monga Mose, ndi Paulo, ndi monga chomwecho, kumutsitsira iye pansi, kuti akapeze ulemelero kuchokera mmoyo wake, ndi kumulola iye kuti akhale wa mndende kwa Mzimu Woyera.

⁵⁸ Tsopano ife tikuzindikira kuti, mfumu iyi, ndi chinthu china chimene ife tikuphunzira apa pa Uziya, kuti, pamene iye anaitanidwa kumeneko ndi munthu amene anali ndi mphamvu yotenga chofukizira, munthu wopatulidwira ku ntchitoyo, pamene iye anamuitanira kumeneko, iye anakwiya naye iye.

⁵⁹ Oh, bwanji—chinthu chotembereredwa bwanji chimene icho chingakhale! Pamene munthu ayesetsa kulozera kwa munthu kuti “Inu mukulakwitsa,” ndi kutsimikizira izo kwa iye mwa Mawu a Mulungu, “Inu mukulakwitsa,” ndiyeno munthuyo, chifukwa chakuti iye akudzimva mwa iyemwini kuti iye achita zomwe akufuna kuchitazo, ndipo sagonjera ku Mawu, ndiye iye amakwiya.

⁶⁰ Inu mukuzindikira chimene chinamuchitikira mfumu? Khate linatulukira pankhope pake pamene iye anali akadali mu mkwiyo wake. Khate linamukantha Uziya pankhope, ndipo ansembe ndi iwo anazindikira izo, ndipo anamuponyera iye kunja kwa kachisi, ndipo iye anafa, wakhate. Moyo wawukulu uja umene unayamba bwino kwambiri, unakathera kukhala wakhate, ndi kuponyeredwa kunja, ndipo ankakhala mnyumba ya yekha, masiku onse a moyo wake, munthu amene moyo umene Mulungu nthawi yina ankawupanga kuti uzikopa.

⁶¹ Ine ndinganene izi, ulemu. Ife tiri nawo amuna lero kumunda, anyamata, ndi amuna a usinkhu wapakati, ndi okalamba, amene anayamba akuthamanga bwino, ndipo anayesetsa, ndipo anapanga chiwonetsero chabwino kwa Mulungu. Koma ife tikuwapeza iwo, lero, kunja uko, zidakhwa, ndipo anashota, ali kunja uko mu zinazo, kutali ndi ife. Ena a iwo anabwerera mmbuyo, limodzi. Ena a iwo achita misala ya ndalama, ndipo ena achita misala ya akazi ndipo akwatira akazi ena omwe sanali akazi awo. Ndipo—ndi zinthu zonsezo ndi chitonzo chomwe chabweretsedwapo, chipembedzo chirichonse. Ife, mmodzi sangakhoze kumutcha winayo woipa, chifukwa ndife tonse olakwa, tonsefe, kapena chipembedzo chirichonse. Ife tawapezapo amuna ngati amenewo, amene nthawi ina anakopedwapo ndi Mulungu ndipo anali nako kukopa kwakukulu kwa anthu. Ndipo komabe pamene iwo anadzimverera okha okwanira . . .

⁶² Pamene munthu apeza malo amene iye angakhoze kumakopa mmalo mwa Mulungu, iye ayenera kumadzichepetsa yekha, nthawi zonse, mowirikiza.

⁶³ Ndipo ife tikupeza kuti, mfumu iyi inafa mwamanyazi, wakhate. Zitatero, iye anali phunziro kwa mneneri wachichepereyo, kuti asamaike ziyembekezo zake pa munthu aliyense, koma kuti aziyang'ana kwa Mulungu yekha. Pamene iye anayamba kuyang'ana kwa munthu kukhala chitsanzo, munthu uyu analephera, komabe atakhala munthu wabwino.

⁶⁴ Chotero ilo ndi phunziro kwa ife, usikuuno, kuti tiziyika malingaliro athu pa Mulungu, mosalabadira kuti munthu wake uti. Kaya iye ndi kardinolo, wansembe, mneneri, chirichonse chimene iye angakhale, iye si woti sangalakwitse ndi—ndi kulakwitsa, ndipo ngakhale imfa, ndi tchimo. Koma alipo Mmodzi Yemwe ali, ndipo ameneyo ndi Yesu Khristu; Iye ndi Mmodziyo.

Mwa ichi, Yesaya anaphunzira phunziro, Mulungu amamulamulira munthu Wake kupita pa malo.

⁶⁵ Munthu alibe ufulu woti aziimirira ndikuti, “Chabwino, ine bwenzi ndikukhala moyo wophweka ngati ndikanakhala mtumiki. Ine ndikukhulupirira ine ndiphunzira utumiki. Ine ndikukhulupirira ine ndichita *izi, izo*, kapena *zinazo*. Ine ndikukhulupirira ngati ine ndingakhoze kutsanzira mphatso iyi imene Mulungu wapereka, iyo ingakhoze . . . Ine ndingakhale ndi misonkhano yokopa anthu ikuluikulu, ndi zina zotero.” Ife tikuwona zochuluka kwambiri za izo lero.

⁶⁶ Koma pamene inu munapeza kuti, Yesaya anapeza phunziro apa, kuti Mulungu amamuyika munthu Wake, Iyemwini. Mulungu amachita kuyikako, ndipo Iye sanamupange konse munthu uyu kukhala wansembe. Iye anamupanga iye kukhala mfumu, ndipo iye ayenera kukhala mfumu. Iye sayenera ayi—

asamayesere... Yesaya anaphunzira apa kuti iwe usamayesere kutenga malo a munthu wina.

⁶⁷ Ndiye pamene iye anawona kuti ngwazi yake yaikulu inafika pa manyazi awa ndipo anapita kumeneko ndipo anakafa, Yesaya anamverera ndiye kuti pafupifupi chiyembekezo chonse cha iye chapita, kotero iye anapita ku kachisi tsiku lina kukakambirana izo ndi Ambuye, ndipo ndi kumene masomphenyawo anachitikira. Ku kachisi, iye anamuwona Mmodzi yemwe iye ankayenera kuti aziyang'anapo nthawi zonse. Mu kachisi, iye, anawona, mmasomphenya, Mulungu atakhala pamwamba pa mpando wachifumu, atakwezedwa pamwamba Mmiyamba, ndipo ulemelero Wake unali ndi Iye. Masomphenya awa iye anawawona, pamwamba, atakwezedwa mmwamba, mpandowachifumu Wake, pamwamba pa ulamuliro uliwonse wa padziko lapansi. Mulungu, ndiye Mmodzi yemwe iye ankayenera kumayang'anapo, pamene iye anali mmasomphenya.

⁶⁸ Ndiyeno ife tikuzindikira izi, kuti Aserafi Akumwamba anali akuwulukira mmbuyo ndi mtsogolo, mu kachisi. Tsopano, Aserafi, kwenikweni mawu Achihebri pamenepo ndi *Owotcha*. Iwo anali Mmodzi Amene ankapereka zofukizira ndi nsembe. Ndi dongosolo lapamwamba chabe la Angelo, limene—limene limapanga njira kwa wochimwa, bola ngati pali nsembe. Ndipo Aserafi awa, makamaka, Owotcha awa anali ndi udindo wapadera, Iwo amakhala mu Kukhalapo komwe kwa Mulungu. Iwo ndi chimodzimodzi ndi Akerubi, ndipo Iwo anali kumene mu Kukhalapo kwa Mulungu.

⁶⁹ Ndipo pamene mneneri uyu anamverera Mzimu wa Mulungu pa iye, ndipo Iye anatsegula maso ake, inu mwaona, iye anabadwira *kwambiri* cholinga chimenecho, kuti pamene Iye anatsegula maso ake zinali ngati kugwa kuchokera apa kukalowa mdziko ngati kuti iye amalota. Ndipo iye anawona mpando wachifumu wa Mulungu utakwezeka mmwamba *kwambiri*, ndipo kenako iye anayang'ana mu kachisi, ndipo Aserafi awa anali akupita mmbuyo ndi mtsogolo, kudutsa mu kachisi, akufuula, “Woyera, woyera, woyera, ndi Ambuye Mulungu! Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu!”

⁷⁰ Ndi kusintha bwanji, ndipo ndi chikoka chotani ichi chiyenera kuti chinali pa mneneri wachinyamata uyu! Pamene iye anawona kulephera kwa munthu, ndipo ngakhale anthu abwino amalephera, koma tsopano iye akumuwona Mulungu, ndipo iye anawawona Aserafi awa.

⁷¹ Ndipo zindikirani chophimba chapadera chimene Aserafi awa anali nacho. Iwo anali ataphimbidwa ndi mapiko awiri pamwamba pa nkhope Zawo, mapiko awiri pamwamba pa mapazi Awo, ndipo Iwo anali akuwuluka ndi mapiko awiri. Mulungu ali palimodzi woyera. Taganizani za zimenezo,

ngakhale Angelo ayenera kuphimba nkhope Zawo zoyera, kuti akayime mu Kukhalapo kwa Mulungu.

⁷² Ine ndikudabwa, m'bale wanga, ine ndikudabwa, mlongo wanga, ngati ife tingayang'ane pa zimenezo! Pamene, Angelo oyerayenera kuphimba nkhope Zawo, kuti akayime mu Kukhalapo kwa Mulungu, molemekeza ndi mwaulemu. Koma lero ife timapeza anthu amene amadzitcha okha Akhristu, ngakhale, alibe kulemekeza nkomwe kwa Mulungu, kapena Mawu Ake, kapena anthu Ake, kapena utumiki Wake, kapena kalikonse. Kodi iwo adzachokera kuti mu chiukitsiro? Baibulo linati, “Ngati olungama adzapulumutsidwe movutikira, kodi wochimwa ndi wopandaumulungu adzawonekera pati nkomwe?”

⁷³ Ndipo pamene, Aserafi, dongosolo lapamwamba kwambiri la Angelo, pafupi ndi Mpando Wachifundo pomwe, Owotcha nsembe, ankayenera kuphimba nkhope Zawo zoyera, kuti ayime mu Kukhalapo Kwake, ndipo apa Iwo anali. Mulungu atakhala pamenepo pa Mpandowachifumu Wake, ndipo Akerubi awa akupita mmbuyo ndi mtsogolo, akufuula, usana ndi usiku, “Woyera, woyera, woyera, ndi Ambuye Mulungu!” Kodi inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza? Zindikirani. Iwo, mapiko awiri, Iwo ankaphimba nkhope Zawo. Ndipo bwanji?

⁷⁴ Ife tikuzindikira lero, kuti, chifukwa chakuti anthu ali...alibe kulemekeza. Iwo amabwera ku tchalitchi, anthu amabwera ku tchalitchi, ndipo—ndipo amadulira, ndi kuseka, amayankhula, amaseleula, atakhala pamene Uthenga ukulalikidwa, opanda kulemekeza nkomwe. Ndipo akakumana nawe pa msewu, ndipo ndi...Iwe sumayembekezera ulemu uliwonse kuchokera kwa anthu; ife tisamachite zimenezo. Komabe izo—izo zimasonyeza ulemu Wachikhristu ukamayetsa kuwalemekeza anthu, kunena kuti, “Mmawa wabwino, m'bale,” kapena chirichonse chimene inu mukufuna. Ena a iwo amakuwa, “Moni, Lalikani!” Oh, izo ndi zawamba kwambiri.

⁷⁵ Kumbukirani, Yesu anati, “Monga inu mwachitira kwa awa, inu mwachitira izo kwa Ine. Iye amene andilandira Ine, alandira Iye amene anandituma Ine. Ndipo iye amene amulandira Iye amene Ine ndamutuma, amulandira Iye. Onani, pamene inu mukuchitira kwa iwo, inu mwachitira izo kwa Ine.”

⁷⁶ Ndipo kupanda ulemu, inu mukudziwa chimene izo ziri? Ndizo...Iwo samakuzindikira Kukhalapo kwa Mulungu. Dziko lakhala la—lawamba kwambiri, ndipo chipembedzo chadzakhala chotsika kwambiri, mpaka palibe kulemekeza, basi monga momwe izo zimakhallira nthawi zonse.

⁷⁷ Tayang'anani pa asilikari amenewo. Ife tikhoza kulingalira, usikuuno, chinali chinthu chopanda nzeru komanso choyipa kuti asilikari amenewo ayike chi—chinsanza pa nkhope ya

Ambuye wathu Yesu, kumusereula Iye chifukwa chokhala Mneneri ndipo amakhoza kudziwa zinsinsi za mu mtima. Iwo anaika chi—chinsanza pa nkhope Yake, ndipo anamukhazika Iye kunja uko pabwalo la milandu, ndipo anatenga ndodo ndipo anadzamukantha nayo Iye pa mutu, ndiyeno anapatsirana wina ndi mzake, ndipo anati, “Ngati Iwe uli mneneri, losera tsopano, tiuze ife mmodzi wa ife yemwe wakumenya Iwe.” Mwaona, palibe kulemekeza nkomwe. Iwo sakanakhoza kumverera ukoma.

⁷⁸ Koma mkazi wamng’ono uyo, ndi chikhulupiriro chokwanira chimene chikanakhoza kukhudza chovala Chake, iye anapeza zokhumba zake. Inu mwaona, ife tiyenera kukhala, ife tiyenera kukhala ozindikira Kukhalapo kwa Mulungu.

⁷⁹ Zokhudzira faivi zazing’ono izi zimene ife tikukhalamo, ndizo dziko laling’ono chabe la ifeeni. Mukuona? Koma Mulungu... Ndizo, ife tinangopatsidwa izi kuti ife tizikhoza kulumikizana ndi dziko lathu lapansi. Koma ziripo zokhudzira kupitirira izo, madera ena.

⁸⁰ Ndipo Mulungu nthawizonse amakhalapo. Ngati ife tingakhoze kokha kukumbukira zimenezo. “Angelo a Ambuye amazinga mozungulira iwo amene akumuwopa Iye.” Mchipinda chino, usikuuno, mwayima Yesu Khristu. Mchipinda chino usikuuno muli makamu a Angelo, masauzande a Iwo asonkhana mozungulira. Inu simukuwawona Iwo, koma inu mukhoza kumverera kukopa kwa Iwo, zikukuuzani inu kuti Iwo ali pano. Ngati izo siziri chomwecho, ndiye Lemba siliri chomwecho. Ndipo ngati Lemba siliri lolondola, ndiye Mulungu si wolondola. Baibulo linanena kuti, “Angelo a Mulungu amazinga,” Iwo samachoka, “Iwo amakhala pafupi ndi iwo amene amamuwopa Iye.”

⁸¹ Yesu anati, “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati pawo.” Ndiye izo zimamupanga Iye mdziko limene ife sitingakhoze kuliwona, limene zokhudzira zathu faivi sizimagwirako. Yesu Khristu ali pano, alipo. Ngati ife tingakhoze kukhala ozindikira za izo!

⁸² Ndipo, kumbukirani, osati pano pokha, koma pamene iwe ukuyenda mumsewu, kulikonse kumene iwe uli, inu amene mumadzinenera kukhala okhulupirira ndi kuti mumamuwopa Ambuye, kumbukirani, Angelo a Mulungu akuyenda nanu kulikonse kumene inu muli. Iwo amapenyerera chirichonse chimene inu mukuchita, lingaliro lirilonse limene limadutsa mmalingaliro anu, ndipo Iwo amadziwa zonse za inu. Chotero, ife tiyenera kukhala ozindikira zimenezo.

⁸³ Ngati sitikuzindikira za zimenezo, ndiye inu mumachita mwanjira iliyonse. Chotero anthu makamaka, lero, anthu ochuluka kwambiri, sakuzindikira za Kukhalapo kwa Ambuye

Yesu, ndi chifukwa chake (iwo) ife tiri nazo zinthu izi zimene ife tiri nazo zikuchitika tsopano, izo si zolondola.

⁸⁴ Ngati ife titangochita monga Davide ananenera, “Ine ndimawayika Ambuye nthawizonse patsogolo panga.” Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. “Ambuye nthawizonse amakhala patsogolo panga. Kumene Iye akupita, ine ndimamutsatira. Ndipo ine ndimadziwa zimenezo kulikonse kumene ndikupita,” mawu ena, Davide anati, “kuti Ambuye ali patsogolo panga.”

⁸⁵ “Ine sindidzakusiyani inu kapena kukutayani inu,” anatero Yesu. “Onani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, mpaka kumapeto kwa dziko lapansi.” Iye sangakhoze kutisiya ife. Iye analonjeza kuti sadzatero.

⁸⁶ Ndicho cholinga chenicheni cha misonkhano iyi. Ndicho cholinga, abale anga, chotengera utumiki wanga kuchoka ku zipembedzo, ndi kuyesetsa kuti ndiwalole anthu awone kuti Yesu Khristu akadali wamoyo, ndipo Iye ali pano, kwa wokhulupirira aliyense, kwa chipembedzo chirichonse chimene chiti chidzamukhulupirire Iye. . . kapena anthu mu zipembedzo zimenezo. “Ambuye ali patsogolo panga,” Davide anati, “ndipo ine sindidzagwedezeka.”

⁸⁷ Zindikirani tsopano, ndi mapiko awiri Iwo anali nawo ataphimba pa nkhope Zawo, kuti ayime mu Kukhalapo kwa Mulungu, chifukwa ndiko kumene Iwo ankatumikira.

⁸⁸ Ndipo ngati Iwo ankachita kuphimba nkhope Zawo zoyera, kuti azitumikira kwa Mulungu, kodi ndi munthu wamtundu wanji yemwe mlaliki akuyenera kukhala? Momwe ife tiyenera kuphimbira nkhope zathu, mwamanyazi! Momwe ife tiyenera kukhalira moyo! Mulungu palimodzi ndi woyera. Ife tiyenera kuzindikira, nthawi zonse, kumakumbukira zimenezo. Kunja kwa chisomo cha Mulungu, ndife ochimwa amaliseche, koma Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife ku tchimo.

⁸⁹ Tsopano Iwo anali ndi mapiko awiri ataphimba mapazi Awo. Izo zikuimira kudzichepetsa.

⁹⁰ Monga Mose, Mose sanali wodzichepetsa kwambiri mpaka atakumana ndi Mulungu mu chitsamba chonyeka moto chija. Koma pamene iye anawona moona kuti uyo anali Mulungu, ndipo chifukwa Kuwala uku kumayankhula mawu a lonjezo (Kodi inu muzikumvetsa zimenezo?), iwo anadziwa ndipo Mose anadziwa kuti nthawi inali itayandikira ya chiwombolo ichi. Ndipo apa pakubwera Chinthu chazimu chikutsika, ndi chikubwereza, ndi kuti, “Ine ndikukumbukira lonjezo Langa kwa Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo.” Ndipo Mose anavula nsapato zake, kudzichepetsa, maziko ake onse. Iye anavula nsapato zake.

⁹¹ Paulo, pamene iye anawona Mngelo yemwe uja wa Kuwala pamwamba pa iye, ndipo anachitcha icho “Ambuye,” iye anagwera mu fumbi la dziko lapansi. Iye anazindikira. Kudzichepetsa, “Ine sindirinso kanthu!”

⁹² Nzosadabwitsa kuti Yesaya anakhoza kulira, “Tsoka ndi ine, pakuti ine ndaona Ambuye Mulungu wa makamu.” Komabe, ali mneneri!

⁹³ Ndipo komabe, Paulo, pokhala munthu wamkulu, sikolala, koma pamene iye anabwera mu Kukhalapo kwa Mulungu, iye anadzichepetsa yekha.

⁹⁴ Ndipo pamene Mose anabwera mu Kukhalapo kwa Mulungu, iye anadzichepetsa yekha. Iye anali mneneri. Iye ankalemekeza Mulungu, Mawu.

⁹⁵ Zindikirani, Yohane M’batizi, pamene Yohane anayima pa gombe atatha kuwabatiza anthu ndipo anayang’ana kunja ndipo anawona Kuwala komweko kukutsika kuchokera Kumwamba, iye anafuula, “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi!” Ndipo pamene iye anadzichepetsa yekha, ndipo, Yesu anatulukira kukalowa mmadzi pafupi ndi iye.

⁹⁶ Tsopano apa pali funso lomwe ndinafunsidwa ine tsiku lina. Izo zikhoza kubwera mu malingaliro anu. Pamene Yesu anayenda kukalowa mmadzi, ndipo Yohane anati, “Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi Inu, ndipo bwanji Inu mukubwera kwa ine?”

⁹⁷ Tsopano, m’bale wanga wakale wa Chibaptisti, Dokotala Roy Davis uja, anakonda kundiuza ine. Iye anasanjika manja ake pa ine pamene iye anandidzoza ine mu mpingo wa Missionary Baptist. Iye anati, “Billy, chachitika ndi chiyani...” Ine ndinamufunsa iye za zimenezo. Iye anati, “Apa pali chimene chinachitika. Inu mukuona, Yohane anali asanabatizidwepo, iyemwini, chotero Yesu anamubatiza Yohane. Ndiyeno Yohane anatembenuka ndipo anabwerera, nakamubatiza Yesu, chifukwa Yesu sakanakhoza kumubatiza Yohane Iye asanabatizidwe.” Chabwino, ine ndinkaganiza izo zimamveka bwino.

⁹⁸ Koma tsiku lina, pafupifupi zaka ziwiri zapitazo, uko mu nkhalango kumene ine ndinali nditakhala, Mzimu Woyera unadzatsika, Kuwala, ndiyeno ine ndinawona chimene icho chinali, pamene Iye anachiwulula icho.

⁹⁹ Tsopano apa pali chimene icho chiri. Mwaona, apo panali anthu awiri ofunika kwambiri pa dziko lapansi: apo panali Yohane mneneri; apo panali Yesu Mesiya. Ndipo iwo, awiri, mwa amuna amene anali nawo Uthenga wa tsikulo, anakumana maso ndi maso mmadzi, pamene maso awo anayang’anizana wina ndi mzake. Ndipo Yohane, modzichepetsa, anati, “Ine ndikusowa kubatizidwa ndi Inu, ndipo chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

¹⁰⁰ Yesu anati, “Balola kuti izo zikhale chomwecho.” Ndiko kulondola. “Koma icho chikutiyenera ife, kapena izo ziyenera kwa ife...” *Behooveth* amatanthauza “kuyenera.” “Ndi

koyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.” Chifukwa chiyani? Yesu pokhala Mulungu; Yohane pokhala mneneri. Mwamsanga Yesu anadziwa pamene Iye ananena kuti, Yohane pokhala mneneri kwa yemwe Mawu ankabwerako, ankadziwa kuti iye akanadzamvetsa izo. Chifukwa, nsembe, molingana ndi lamulo, inkayenera kuti itsukidwe iyo isanaperekedwe. Ndipo Yesu ankayenera kuti abatizidwe asanaperekedwe. Iye anati, “Balola kuti izo zikhale chomwecho tsopano. Uko nkulondola. Pakuti kotero zikutiyenera ife, kuyenera kwa ife kukwaniritsa chirungamo chonse.”

¹⁰¹ Oh, ngati ife tingakhoze kutenga izo ngati mutu kwa maminiti pang’ono! Zomwe ife tikuziwona lero, monga—monga okhulupirira mu Kuwala mu ora limene ife tikukhalamo, ndikoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Izo zikukhala kwa mpingo wa pentekoste, kuti ife tikwaniritse chirungamo chonse, powona kuti ife tinayitanidwa ndi Mzimu Woyera. Ndi zosayenera kuti ife tidzilekanitse tokha kwa abale ena. Ndi zosayenera kuti ife tizidzipanga tokha chipembedzo ndipo sizikhala ndi china chochita ndi m’bale wathu yemwe walandira Mzimu Woyera mofanana ndi momwe ife tinachitira. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Izo sizikuyenera kwa ife. Pamene tikumuwona Mulungu akuyenda ndi kumachita, ndi kuchita ndendende zomwe Iye ananena, ndipo chifukwa munthuyo si wolumikizana ndi bungwe lathu, kuti ife timachita moyerekedwa, zimenezo ndi zosayenera. Izo si zolondola.

¹⁰² Ife tiyenera kukhala Akhristu. Ife tiyenera kukhala njonda. Ife tiyenera kukhala anthu owopa Mulungu ndi amuna. Ife tiyenera kukhala okonzeka kukafikira tsidya linalo ndi kumupatsa munthu aliyense chanza, ndi kutambasulira bulangeti kumbali yake ya bedi, aponso. Inde, pakuti zikutiyenera ife kukwaniritsa chirungamo chonse. Tsopano ife tikudziwa. . .

¹⁰³ Izo zinali chifukwa chakuti Iye anali Nsembe. Ndipo Yohane anadziwa izo, chifukwa iye anakuwona Kuwala kuja pa Iye. Ndipo Yohane anadzichepetsa yekha, pokhala munthu wamkulu kwambiri mpaka ora limenelo. Koma pamene iye anawawona Ambuye Yesu wamkulu uyu akubwera, iye anati, “Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi Inu.”

¹⁰⁴ Koma pamene Iye anamuza iye, “Izo zikutiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.”

¹⁰⁵ Ndiye Yohane anatembenuka, akudziwa, monga wantchito wa Mulungu, monga mneneri, iye ayenera kukwaniritsa Mawu a ora limenelo, chifukwa iye ankadziwa kuti Iyo inali Nsembe. Iye anali atangonena chomwecho, “Apo pakubwera Mwanawankhosa wa Mulungu, Mwanawankhosa wansembe yemwe ati achotse machimo a dziko lapansi.” Ndipo

Mwanawankhosa ankayenera kuti atsukidwe mu mphika iye asanaperekedwe kwa wansembe. Amen.

¹⁰⁶ Ndikoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse, pamene inu mutenga pa Dzina la Yesu Khristu. Mulole mwamuna kapena mkazi aliyense, amene atenga Dzina la Yesu, achoke ku tchimo.

¹⁰⁷ Kuvomereza kwathu lero kwayamba kumabwera monga ngati a—a ine-sindikudziwa-chiyani, mwambi wina kapena chinachake. Ife timapita kumeneko ndi kukapemphera pemphero pafupifupi utali wa maminiti awiri, ndipo ndikudzukapo; tikachita chinachake cholakwika, kunena kuti, “O Ambuye, Inu mukudziwa ine sindimafuna kuti ndichite zimenezo, koma, aleluya, ine ndiri bwino,” nkumapitirira. Ayi, sindizo zimenezo, m’bale.

¹⁰⁸ Inu muyenera kukhala wachisoni mwaumulungu. Inu muyenera kuchivomereza chinthucho. Inu muyenera kuchikonza icho. Inu simungakhoze kuchita izo... Yesu anati, “Pamene inu mupita ku guwa, mukakumbukira kuti m’baleyo ali ndi kanthu kotsutsa inu, mupite kwa iye choyamba inu musanadzapereke mphatso yanu pano, mukayanjanitsidwe ndi m’baleyo.” Mukuona? Ndi chotiyenera ife, kwa ife, kuti ife tikwaniritse chirungamo chonse.

¹⁰⁹ Ndipo akazi inu a tsitsi lalifupi, lodula, kodi inu mukudziwa chiyani? Ndi choyenera kwa inu kuti muzilola tsitsi lanu lizikula ndikumachita ngati dona. Inu amene mumavala akabudula; achotseni iwo, zivalani madiresi. Ndi choyenera kwa inu kuti inu muzichita monga Akhristu, ndiko kulondola, chifukwa Baibulo linati izo nzolakwika. Mkazi sayenera kumachita zimenezo.

¹¹⁰ Ndipo amuna inu amene mukusuta ndudu, izo nzosayenera. Ndipo amuna inu amene mumawalola akazi anu kumachita zimenezo, ndiyeno nkumati kuti ndinu “ana a Mulungu,” mwamuna?

¹¹¹ Lalikulu, lumbiriro lalikulu limene limatengedwa pamwambo wa chikwati, “chikondi, ulemu, ndi kumvera,” linapita. Mu America, mkazi amakhala ndi ufulu woyambirira kupita. Chabwino, kulikonseko iye amakhala ndi ufulu woyambirira kupita. Baibulo linati iye akanadzakhala nazo izo mwanjira imeneyo.

¹¹² Iwo amanena kuti akazi ndi oyendetsa mosamalitsa kwambiri omwe ife tiri nawo mdziko muno. Izo nzolakwika. Mwana wanga ndi ine, timadutsa fukoli, mmbuyo ndi mtsogolo, timasunga kalemba, ndipo nthawi iliyonse pakakhala chomwe ife timachitcha kujejemetsana pa msewu, ngati ali mwamuna ife timaika icho pansu pa mwamuna, ndi mkazi pansu pa mkazi. Ndipo pansu pa kujejemetsana firii handiredi kudutsa fukoli, pamakhala thuu hndiredi ndi eyite wani a akazi amenewo.

113 Kodi zawozo anazitenga pati? Chifukwa cha ma ripoti omwe anaperekedwa. Ndithudi, apolisi amenewo sangawagwire akazi owoneka bwino amenewo ngati iwo atenga nambala yafoni. Iwo sangawamange iwo. Iwo amawasiya iwo azipita, ndipo ndicho chifukwa chake.

114 Inu mukuona, ilo lasanduka dziko la akazi. Baibulo linati izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo. Ndendende. Chotero mlaliki pa guwa ali basi pafupifupi chinthu chomwecho, iye amachita mantha kunena chirichonse chotsutsa izo.

115 Koma ndi chotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Izo ziyenera kunenedwa penapake. Iwe sumayang'ana pa kutchuka kwanu ndi kutchuka pano. Iwe ndi—iwe ndi wandende wachikondi ku Uthenga wa Yesu Khristu, ndinso wokakamizidwa. Ndiwe wamndende kwa Iye, ndipo iwe sunganene china chirichonse koma chimene Mzimu Woyera ukunena, ndi kulalikira chinthu chimene chiri cholondola. Kulondola. Iwe umakhala wamndende wa chikondi kwa Iye. Ndiye iwe sumasala chomwe icho chiri, inu umayenera kukwaniritsa chirungamo chonse. Mtumiki ayenera kuyankhula zimenezo, inu anthu Achipentekoste makamaka, amene—amene mumadziwa bwinoko kusiyana ndi—kusiyana ndi kuti izo zizipitirira monga chomwecho.

116 Tsopano kuno nthawi ina kale, munthu wamkulu wotchuka anabwera kwa ine, anati, “Bwanji inu osawasiya akazi amenewo okha?” Anati, “Bwerani kuno, ine ndikufuna kuti ndisanjike manja pa inu ndi kukupemphererani inu, kuti muzipitirira, ndi kumangopempherera odwala.” Anati, “Bwanji, anthu amakutengani inu ngati mneneri.”

Ine ndinati, “Ine sindinayambe ndanenapo kuti ine ndinali mneneri.”

117 Iye anati, “Koma anthu amakutengani inu monga choncho.” Anati, “Inu mukuyenera muziwaphunzitsa anthu amenewo momwe angapezere mphatso zazikulu zauzimu.”

Ine ndinati, “Ndiro lomwe liri vuto ndi mpingo lero.”

118 Anati, “Osati kuwauza iwo za kudula-tsitsi lawo, ndi *izi, izo, zinazo*. Ine...” Anati, “Inu muyenera kumawaphunzitsa iwo zinthu zazikulu, zapamwamba.”

119 Ine ndinati, “Ine ndingakhoze bwanji kuwaphunzitsa iwo algebra pamene iwo sangaphunzire nkomwe ma ABC awo?” Uko nkulondola.

120 Iwe umayenera kuyambira penapake, kotero umapita pansi ndipo umakamanga chomakwera. Musadzayesere kuyambira pamwamba; inu mulibe maziko aliwonse. Ndipo ndiro limene liri vuto ndi zimenezo lero, abale, iwo samatenga Ichi, “Izo zikutikakamiza ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.”

Zindikirani Angelo awa tsopano.

¹²¹ Ndipo Yohane M'batizi, Paulo, ena osiyanasiyana, pamene iwo anawona Ulemelero wa Mulungu uja ndi Kuwala kuja, iwo anagwadira kwa Iwo. Iwo, inde, iwo analemekeza Iwo, iwo analemekeza Iwo, chifukwa chakuti iwo ankadzichepetsa okha.

¹²² Ndipo Angelo awa, mpakana, amene amatumikira mu Kukhalapo Kwake, anaphimba mapazi Awo ndi kuphimba nkhope Zawo. Oh, mai! Tsopano zindikirani, mwamsanga tsopano, Iye anali nawo mapiko ena awiri, ndipo, mwa ichi, Iye akanakhoza kudziyika Yekha mu kuchitapo.

¹²³ Tsopano ndi wantchito weniweni bwanji ameneyo, wa Mulungu, amadziwa, amamusonyeza mneneri momwe wantchito Wake wokonzeka ayenera kukhalira. Kodi wantchito wokonzekera ayenera azikhala chotani? Tsopano antchito awa amayang'ana pa . . . Iye anali atayang'ana pa a—munthu padziko lapansi apa ndi kuwona kulephera kumene iye anapanga, zitatero Mulungu anamuwonetsa iye Ufumu Kumwamba, mpandowachifumu. Ndiye Mmodzi woti uziyang'anapo. Ndiye Iye anamusonyeza iye chimene wantchito weniweni ayenera kukhala, yemwe ankatumikira mu Kukhalapo Kwake. Ndipo apa panali Aserafi awa, ndiye, anaphimba nkhope Zawo zoyera, anaphimba mapazi Awo, ndipo ndi mapiko awiri Iwo anapita mu kuchitapo; molemekeza, modzichepetsa, ndipo ndikumagwira ntchitoyo. Amen. Ngati ameneyo si wantchito wovala-bwino, ine sindikudziwa chomwe chiri; wolemekeza, wodzichepetsa, ndipo akugwira ntchito. Oh, mai! Ine ndikukuuzani inu!

¹²⁴ Monga mkazi wamng'ono pa chitsime, pamene iye anazindikira mphatso ya Mulungu ija, ndipo Munthu uyu amene anayankhula anali Mesiya, izo ndithudi zinamuyika iye mu kugwira ntchito mwamsanga ndithu. Iye anayiwala za mtsuko wake wamadzi. Iye anathamangira mu mzinda, akuti, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Yemwe wandiuza ine zinthu zomwe ine ndazichita. Kodi Uyu si Mesiya yemwe?” Oh, analowa mu kuchita kotani iyeyo!

¹²⁵ Petro, pamene anamutenga Iye pa Mawu Ake, monga ife tinali kuyankhulira mmawa uno, kunja uko mu ngalawa. Kodi inu munazindikira? Pamene Petro anatenga Mawu Ake, ndipo anagwetsera ukonde pansi mmenemo, ndipo anagwira—kulemera kwakukulu kwa nsomba, unyinji wa nsomba, mwamsanga Petro anasiya ukondewo ndipo analowa mu kuchitapo. Iye asanachite zimenezo, iye anagwa pansi pamaso pa Ambuye, ndipo anati, “Chokani kwa ine, O Ambuye, ndine munthu wochimwa.”

¹²⁶ Ngati amenewo si mawu omwewo, monga, amene Yesaya mneneri ananena, “Tsoka ndi ine, pakuti ine ndawawona Ambuye Mulungu, ndipo ndine munthu wa milomo yonyansa.”

¹²⁷ Kodi inu simukuwona chimene Kukhalapo kwa Ambuye kumachita kwa okhulupirira enieni? Ife sitimafuna nkomwe

kuti tivomereze; ife timangofuna kunena kuti, “Chabwino, ndife Achipentekoste, ndife Abaptisti, ndife Apresbateria,” nkumapitirirabe ndi moyo. Koma weniweni, wantchito wa Mulungu woitanidwa, amadzichepetsa yekha mu Kukhalapo kwa Mulungu. Iye samawatsutsa Iwo.

¹²⁸ Taonani amene ankamutsutsa Ambuye Yesu, anali Afarisi, mipatuko, iwo anali omwe ankamutsutsa Iye.

¹²⁹ Koma munthu amene anali wofunitsitsadi kukhala mtumiki Wake, anadzichepetsa yekha ndipo analowa mu kuchitapo. Yesu anati, “Inu mudzanditsatira Ine, ndipo Ine ndidzakupangani inu asodzi a anthu.” Pamene iye anawona kuti Ameneyo analidi Mulungu, iye anapita mu kuchitapo.

¹³⁰ Munthu wakhungu yemwe anachiritsidwa, Baibulo linanena kuti iye “anamwaza kutchuka Kwake kudutsa dziko lonselo.” Iye analowa mu kuchitako pamene iye anapeza kuti Mulungu anali ndi Womuimira kuno pa dziko lapansi, amene akanakhoza kutsegula maso a munthu wakhungu, ndi kupita kozungulira akuchitira umboni, kupereka matamando kwa Mulungu. Ndipo Afarisi anamugwira iye, ndipo chimene chikanati chikhale kwa iye, ndipo monga ine ndinanena mmawa uja. “Bwanji,” iye anati, “Ine sindingakhoze kufotokoza, kutsutsana fioloje ndi inu. Koma chinthu chimodzi ichi ine ndikuchidziwa, momwe ine nthawi ina ndinali wakhungu, ine tsopano ndikupenya.” Iye analowa mu kuchitapo, ndithudi, chifukwa iye anali atamwaza kutchuka Kwake kulikonse.

¹³¹ Ndipo, nthawizina, mwinamwake sindinu mtumiki, kumwaza kutchuka Kwake, koma moyo wanu udzamwaza kutchuka Kwake ngati inu mungokhala moyo woyenera.

¹³² Anthu osauka pa Pentekoste, gulu lija la asodzi ndi—ndi okhometsa msonkho, ndi ena otero, okhala ndi ntchito zonyozeka. Iwo anapita kumeneko pa lonjezo la Mulungu, ndipo iwo anakadikirira mu chipinda chapamwamba kwa masiku teni. “Ndipo mwadzidzidzi kunamveka mkokomo wochokera Kumwamba ngati mphepo yamkokomo, inadzaza nyumba yonse imene iwo anakhalamo.” Ndipo iwo anachitapo kanthu, chifukwa chakuti iwo anali atawona lonjezo la Mulungu likuwonetseredwa. Ilo linatsimikiziridwa kwa iwo, lonjezo la Mulungu, ndipo ilo linawayika iwo mu kuchitapo. Pamene lonjezo Lake linakwaniritsidwa, ilo linawayika iwo mu kuchitapo.

¹³³ Mzanga, ine ndinene izi. Zimene ife taziwona mu chaka chathachi kapena ziwiri, mu Ufumu wa Mulungu, ziyenera kumupangitsa Mkristu aliyense wobadwanso mwatsopano kulowa mu kuchitapo. Koma chinthu chake ndi chakuti, ife siti—ife sitimachilemekeza icho, kuzindikira kuti ndi Mulungu. Ndife—ife timangochita chidwi pang’ono. Ife timafuna kuwona zinthu zazing’ono, ndi kupereka kumverera. Ife timakonda

kumva bwino. Ife timakonda kuchita zinthu izi. Koma pamene zifika pakuzilemekeza kwenikweni Izo ndi kuzikhulupirira Izo ndi mtima wathu wonse, izo zimatiyika ife mu kuchitapo.

¹³⁴ Chabwino, pamene Mngelo anakumana ndi Maria mmawa umenewo panjira yopita ku chitsime, ndipo anamuuzza iye kuti “adzakhala ndi Mwana, osadziwa mwamuna,” izo zinamuyika iye mu kuchitapo. Iye anapita mofulumira, akuwuza aliyense kuti iye “adzakhala ndi Mwana, wosadziwa mwamuna.” Iye sanasamale zimene zinkatanthauza pa zimene anthu ankanena. Iye anali atakomana nayedi Mngelo wa Mulungu, ndipo izo zinamuyika iye mu kuchitapo. Iye ankadziwa kuti Mzimu Woyera unali pa iye, ukulenga mwa iye Moyo.

¹³⁵ Oh, ngati ife tikanakhoza kokha kuzindikira chimenecho, kuti Mzimu Woyera uli pa ife, ukulenga mwa ife chikhulupiriro, kuyesera kuti adziwonetsere Yekha mu njira zambiri zosiyanasiyana ndi mphatso, kuti alenge chikhulupiriro cha Mpingo wokwatulitsa. Izo ziyenera kutiyika ife mu kuchitapo kanthu. Koma ndikudabwa ngati ife tikungozichita izo momwe Iye ankafunira, ndi mwaulemu ndi modzichepetsa?

¹³⁶ Lawi la Moto mmasiku otsiriza ano liyenera kuwuyika mpingo wonse mu kuchitapo, Izo zikutsimikiziridwa, zizindikiro za Kudza Kwake ziri pafupi.

¹³⁷ Israeli wabwerera ku dziko lakwawo. Yesu anati, “Pamene mtengo wa mkuyu udzaphuka masamba ake, mbadwo umenewo sudzatha mpaka zinthu zonse izi zitakwaniritsidwa.” Pamene Israeli akubwerera ku dziko la kwawo ndi kukakhala fuko, m’badwo umenewo udzawona Kudza kwa Mesiya.

¹³⁸ Ine ndinalandira chidutswa chochokera kwa rabbi mu Palestine, tsiku lina, chinali chokhudza kwambiri. Kuli mpesa wawung’ono, chaka chino, wamera mu Palestine umene sunawonekere kumeneko kwa zaka mahandiredi ndi mahandiredi ndi mahandiredi. Ndipo izo zinanenedweratu, ndi Ayuda, kuti pamene mpesa umenewo udzakula kachiwiri, Mesiya adzakhala ali pa njira Yake.

¹³⁹ Amuna anzeru amene anabwera kuchokera uko ku Babeloni, ndipo iwo anali kuphunzira za nyenyezi, iwo anali akasidi. Ndipo pamene iwo ankawerenga nyenyezi, iwo anawona nyenyezi zitatu izi zikufola. Nyenyezi ya Hamu, Shemu, ndi Yafeti, zimene iwo anabadwira pansi pake, ziri mu mzere, ndipo iwo anadziwa. Okhulupirira asayansi amenewo ankawona zolengedwa zakumwamba, momwe iwo zinkayendera, ndipo pamene iwo anawona nyenyezi zimenezo zikubwera mu mzere pa Yerusalemu. Pakuti, ngati iwo anali ku Babeloni, iwo ankayang’ana molunjika kumene cha ku Yerusalemu, cha Kumadzulo, kuti aziwone izo. Ndipo pamene iwo anaziwona izo zikubwera umo, iwo anadziwa kuti pamene nyenyezi zimenezo

zibwera mu mzere ina ndi imzake, Mesiya anali padziko lapansi. Ulemelero!

¹⁴⁰ Ndipo pamene ife tikuwona Israeli akupita kwawo, ndipo Mzimu Woyera ukutsanuliridwa mmipingo, nkhani za ecumenical za kuyendera limodzi, ndi Bungwe la Mipingo, ndi zinthu, ndi Chiroma Katolika ndi Chiprotestanti kugwirizana limodzi, Mesiya adzabwera kudzamutenga Mkwatibwi Wake.

¹⁴¹ Ndipo Mulungu akutumiza mphatso, kuti adzayesere kulenga mwa ife chikhulupiriro chimene chidzatichotse ife pano, tsiku lina, kupita mu Mkwatulo; kuchiritsa odwala, kutsegula maso akhungu, kuwukitsa akufa!

¹⁴² Zizindikiro zazikulu mmwamba kumwamba, Angelo akubwera mu kuwundana! Ndipo asayansi akuyang'ana pa izo, ananeneratu miyezi izo zisanachitike. Ndi zimenezo pamenepo. Ndi zimenezo ziri mu magazini. Anauzidwa miyezi izo zisanachitike! Angelo Seveni anatsika pansi, ndipo anati, "Vumbulutso lathunthu la chinsinsi cha zisindikizo zisanu ndi chimodzi cha Mulungu chidzafutukulidwa." Ndipo apo izo zinali ndendende basi monga Iye ananenera, ananeneratu izo zisanachitike.

¹⁴³ Ndipo iwo anayang'ana pozungulira, iwo anapeza mitundu yonse ya zowoneka zachinsinsi, ndipo anazitcha izo zauzimu za mtundu winawake. Iwo amazitcha izo mbale zowuluka, zizindikiro zowopsya mu mlengalenga, pa dziko lapansi. Zizindikiro, zizindikiro zolozera kwa ife kuti Kudza kwa Ambuye Yesu kwayandikira.

¹⁴⁴ Tsopano mpesa wawung'ono wamera. Israeli ndi fuko lake lomwe. Iye ali ndi fuko lake lomwe, mbendera yake yomwe. Nyenyezi yakale ya nsonga-sikisi ya Davide, mbendera yakale kwambiri padziko lapansi, ikuwuluka kachiwiri, kwa nthawi yoyamba kwa pafupifupi zaka twente-faivi handiredi. Iwo ali ndi ankondo awo awo. Iwo ali ndi ndalama yawo yawo. Iwo ali pafupi... akuimiridwa mu United Nations. Iwo ndi fuko, kwa nthawi yoyamba kwa zaka twente-faivi handiredi. Ndipo pamene iwo anali kusonkhanira mkati...

¹⁴⁵ Ine ndiri nayo tepi ya izo, chithunzi, ife timaitcha iyo *Maminiti Atatu Pasanafike Pakati Pa Usiku*. Ndipo mmenemo, iwo amawafunsa Ayuda awa, akuwabweretsa iwo mmenemo, okalamba, pa nsana wawo, atawabereka iwo. Iwo amati, "Kodi inu munabwera ku dziko lakwanu kuti mudzafe?" "Ayi, ife tikubwera kudzamuwona Mesiya." Amen. Pamene inu muwawona mafunso amenewo, iwo ndi kalendala ya Mulungu, Mesiya ameneyo akukonzekera kuwonekera. Oh, mai!

¹⁴⁶ Ife tiyenera kukhala odzichepetsa. Momwe ife tiyenera kukhala olemekeza! Momwe ife tikuyenera kukhala tiri mu kuchitapo, kuyesetsa kuti tiwupulumutse moyo uliwonse umene

ife tingathe, kumwaza mbewu kuchokera kumanja kupita kumanzere, ndi kuchita chirichonse chimene ife tingathe.

¹⁴⁷ Koma m'malo mwake, ife timati, “Ulemelero kwa Mulungu, ine sindikumverera ngati ndipite usikuuno. Ine ndikukhulupirira, chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndikhala kunyumba ndi kumawonera kuwulutsa kwabwino uku usikuuno. Ndi msonkhano wa mapemphero, koma...” Mpingo wogona, wa Laodikaya, wolemera! Oh, mai! Ndi zimenezotu pamenepo.

Izo ziyenera kutiyika ife mu kuchitapo.

¹⁴⁸ Ife, monga mneneri, tawona kutulukira kwa kudzikweza-okha, zipembedzo. Ife tikuziwona ndendende lero, mu mpingo, zomwe zachitika, monga Yesaya anawonera. Iye anamuwona munthu akulemekezedwa ndi Mulungu, koma ife tinamuwona iye, iye anamuwona iye akudzikweza yekha ndipo anakanthidwa ndi khate. Ife lero, ife tikuwona chinthu chomwecho, cha zipembedzo zodzikweza-zokha, “Ife ndife wamkulu kwambiri wa gululo. Ife tiri nawo mamembala ambiri kuposa ena onsewo.” Kudzikweza-yekha, kuwona khate la kusakhulupirira likuwakatha iwo, ndipo iwo aponyedwera kunja.

¹⁴⁹ Ndiye ife tikanayenera kuyang'anira masomphenya ochokera Kumwamba, omwe angatiwonetse ife Yesu Khristu pakati pathu, Mawu Ake olonjezedwa kuti Iye akanadzachita izo, inde, bwana, kukopedwa osati ndi kachitidwe kena kopangidwa ndi munthu, koma kukopedwa ndi Mulungu Mwiniwake.

¹⁵⁰ Ife tikuwapeza iwo, monga Uziya, anataya kugwira kwawo pa Mawu, chifukwa iwo anasinthanitsa Izo ndi tizikhulupiro, kuyesetsa kudzipanga okha monga Uziya wakale, kuyesetsa kutenga malo a udindo wa wodzozedwa kuseri kwa nsanja, ndi kukana Mawu owona a Mulungu. Iwo alibenso ntchito kumbuyo uko kuposa momwe Uziya anachitira mu zimenezo, pafupi ndi guwa limenero, ndi zofukizira. Munthu amene amadzinenera kuti ndi Mkristu, ndipo nkumakana zoonza za Mawu, alibenso ntchito pa guwa kuposa zomwe Uziya anali nazo izo—ndi chofukizira chimenecho. Munthu amene amadzinenera kuti anabatizidwa ndi Mzimu Woyera, ndi wodalitsidwa ndi Mulungu, ndipo nkuimirira ndi kulikana Baibulo limenelo ndi Choonadi cha Ilo, wasinthanitsa Ilo ndi kachikhulupiro kapena chinachake, iye wangokhala wodzaza ndi khate la tchimo ndi kusakhulupirira monga Uziya anachitira.

¹⁵¹ Iye anachotsedwa pa udindowo, koma iwo amayesetsa kuti akwaniritse udindo umenewo mwa luntha. “Ndine Dokotala Ph.D., LL.D. *Zakuti-ndi-zakuti*.” Onani, iwo amayesetsa kutenga zimenezo ndi kulimbikira maphunziro a kudzoza kwa Mzimu Woyera. Inu mukuona, chotero, munthu akhoza kutenga Baibulo limenelo, ndipo bungwe lina lalikulu likhoza

kuzifotokoza izo ndi kuzigawanitsa izo, ndi kuziyika izo apa ndi kuzikonza izo kuti ziziwoneka zabwino kwambiri kwa inu. Zimenezo ndi luntha. Zimenezo ndi chifukwa chakuti iye anaphunzira ndi kuphunzira, za ngodya izi ndi zinthu, momwe angaziikire izo pamodzi.

¹⁵² Koma ndiloleni ine ndikuwuzeni inu chinachake. Pamene Mulungu abwera pansi mu Mawu Ake, Iye samangowaika iwo pamodzi, Iye amawawonetsera Iwo kunja uko ndi kuwapanga Iwo amoyo, ndipo amawavomereza Iwo ndi kuwatsimikizira Iwo, kuti ndiwo Choonadi. Ndicho Choonadi cha Mawu. Ndi pamene Mulungu Mwiniwake atero.

¹⁵³ Masomphenyawo anamukhudza mneneri. Oh, kukhudza kumene masomphenyawo anachita pa iye! Izo zinamupangitsa mneneri uyu. . .

¹⁵⁴ Tsopano, kumbukirani, iye anakhala akuyang'ana pa munthuyo. Koma pamene iye anadzawona chinachake chenicheni. . . Iye anali atawona moyo woyera wa munthu, iye anamuwona iye akulephera, iye anamuwona iye akutenga khate ndi kufa. Inu mukuyang'ana pa chinthu chomwecho mu zipembedzo zanu. Inu mukuona kumene aliyense wa iwo wapita?

¹⁵⁵ Tsopano kusuntha kwakukulu kwa ecumenical uku. Ngati mpingo sulii mu kusuntha kwa ecumenical uku, mu nthawi ya—yadzidzidzi, mpingo umenewo sudzagwiritsidwa ntchito ngati mpingo. “Ndipo palibe mtumiki adzakhoze kutumikira kwa aliyense, iye adzaphedwa pochita zimenezo. Ngati iye atumikira mdalitso uliwonse kwa anthu akunjia, iyeyo ali ndi kusuntha kwa ecumenical.” Ndizo ndendende mu zolembedwa lero, ndi Achilutera; ine ndayiwa dzina lake. Mwaona, ndiko kulondola. “Tchalitchi chanu simungakhoze kupembedzeramo; icho chidasandutsidwa mosungiramo zinthu.” Onani chilemba cha chirombo chikuyamba kugwira ntchito, ndipo ife tikuyang'ana pa icho. Nthawi, oh, izo ziyenera kuwuyika mpingo mu kuchitapo. Ndithudi, izo ziyenera kutero.

¹⁵⁶ Penyani zotsatira za masomphenya tsopano, zomwe izo zinachita kwa mneneri. Izo zinamupangitsa iye. . . atatha kumuwona munthu ameneyo, ndikuwona izo zikulephera. Anamuwona Mulungu atamukwiya munthuyo, ndipo akuchotsedwa kwa iye, ndipo anamukhantha iye ndi khate.

¹⁵⁷ Kenako iye anatsikira ku kachisi, kuti akati, “Ambuye Mulungu, ine ndikudziwa Inu ndinu Mulungu. Ndipo ine ndakhala ndikuyang'ana chinthu cholakwika.” Ndipo kenako Mulungu anamusonyeza iye masomphenya. Ndipo osati kokha masomphenya, koma masomphenyawo anatsimikiziridwa; chifukwa, pakati pawo panali Aserafi akuwulukira chammbuyo ndi mtsogolo, ndipo ngakhale liwu Lawo linagwedeza nyumbayo pamene ilo limabwera pamodzi, nsanamira za iyo.

¹⁵⁸ Ndiyeno, onani, iye anawona chinachake chenicheni. Ndipo, komabe, iye anali mneneri. Iye anali a . . . Mne—mneneri ndi yemwe Mawu amabwerako. Koma iye anali asanapiteko kudera lina kuposa zomwe iye anali kuyang'anapo, ngwazi yake, Uziya, akuyang'ana pa abusa, a—munthu wamkulu. Ndipo pamene iye anawona kulephera pamenepo, kwa Mawu, ndipo anawawona Mawu akumudzudzula munthuyo chifukwa iye anali akutenga udindo umene iye analibe nawo ntchito kuti akhalemo, ndiye chinadzachitika ndi chiyani? Iye anayang'ana mmwamba, ndipo iye anawawona Ambuye.

¹⁵⁹ Kodi inu mungakhoze kuwerenga pakati pa mizere? Kodi inu mukukhoza kuwona zimene ine ndikunena tsopano? Ambuye Yesu amene analonjeza, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu.” Mulungu yemweyo amene analemba Baibulo, anati, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndipo Iye anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Kodi inu mukumvetsa zimene ine ndikutanthauza?

¹⁶⁰ Ndiye munthu wamtima-woona uja anawona Ulemelero wa Mulungu, iye anawuwona Iwo ukugwira ntchito. Ndipo iye analira, monga wochimwa, ndipo anavomereza yekha kuti anali wochimwa. Iye anali asanawonepo chirichonse chonga chimenecho, chenicheni chomwecho, kale. Iye anavomereza kuti iye anali wochimwa.

¹⁶¹ Ndiye chinachitika ndi chiyani? Pamene mneneri anali atakonzeka kuti avomereze, ndiye panadzabwera kuyeretsa kwenikweni.

¹⁶² Mpaka anthu atakonzeka kuti avomereze, palibe chifukwa chokhalira ndi misonkhano ya machiritso iyi. Ngati inu mutaulula machimo anu, kuvomereza kusakhulupirira kwanu, kuvomereza zinthu zimene inu mukulakwitsa, pamenepo Mulungu akhoza kuchita chinachake. Koma mpaka patakhala kuvomereza, pamenepo sipangakhale kuyeretsedwa.

¹⁶³ Ndipo mwamsanga pamene Yesaya anati, “Watsoka ndi ine! Ndine munthu wa milomo yonyansa, ndipo ine ndikumakhala ndi anthu a milomo yonyansa.” Zitatero panadzabwera kuvomereza, kuti, ndiye panadzabwera Akerubi ndi Moto. Kodi inu munazindikira? Mulungu sanagwiritse ntchito seminare kuti amuyeretse nayo iye. Iye sanagwiritsepo ntchito a—bukhu la malamulo kuti amuyeretse nalo iye. Iye anamuyeretsa iye ndi Moto.

¹⁶⁴ Mulungu nthawizonse amawayeretsa antchito Ake, pamene Iye wakonzeka kuti awayike iwo mu ntchito, mwa Mzimu Woyera ndi Moto. Mulungu amayeretsa ndi Moto; osati ndi mabuku, osati ndi maphunziro, osati ndi lingaliro laluntha, osati

ndi chipembedzo. Koma pogwiritsa ntchito Moto wa Mzimu Woyera, Mulungu amamuyetsa wantchito Wake.

¹⁶⁵ Ndiye zindikirani, ndiye, kutatha kuvomereza, kutatha kuyeretsedwa, ndiye panadzabwera kutumidwa. Ndiye panali kutumidwa. Atatha kuvomereza ndi kuyeretsedwa, ndi pamene Yesaya woyera anamuyankha Mulungu, ndipo anati, “Ndine ine pano, nditumeni ine.” Iye atatha kuyeretsedwa, kuvomereza, kuyeretsedwa ndi Moto, ndiye Yesaya woyera uja anali wokonzeka kugwira ntchito. Iye anali wokonzeka kuti akhale chitsanzo. Iye anali wokonzeka kuti—kuti awuwonetsera moyo wake, kuti ena akhoze kukopeka ndi iye.

¹⁶⁶ Koma kufikira iye atavomereza izo, kufikira iye atayeretsedwa, ndiye kuti iye anali chikoka chosauka kwambiri, monga chidole cha mfumu.

¹⁶⁷ Tsopano iye wayeretsedwa, tsopano iye wavomereza ndipo wayeretsedwa, ndipo waitanidwa ndipo watumidwa kuti akhale mneneri. Ndipo Mulungu anamulola iye alembe Baibulo lonse, mu Mabuku sikisite-sikisi a Baibulo, ilipo mitu sikisite-sikisi ya Yesaya. Iye akuyambira mu Genesis; pakati pa Bukhu panadzabwera Yohane M’batizi; ndipo akupita mpaka mu ulamuliro wa Zakachikwi, mu Yesaya 65 ndi 66, ndiko kulondola, Chivumbulutso. Iye analemba kufokotoza konse kwa Baibulo. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anadzichepetsa yekha pamene iye anawona Kukhalapo kwa Mulungu.

¹⁶⁸ Kodi iye anachita chiyani? Ndipo ake, atatha kuchita zimenezo, ndipo anadzichepetsa yekha ndipo anayeretsedwa ndipo anayikidwa pambali, ndipo anayeretsedwa ndipo anatumidwa, iye wakopa mamillioni a anthu. Apa pali Bukhu lake, apa pali Zolemba za Yesaya zomwe zakopa anthu kuyambira nthawi imeneyo mpaka pano. Chikoka chake chikupitirirabe.

¹⁶⁹ Baibulo linati, “Ntchito zawo zimawatsatira iwo.” Monga Mzimu Woyera unamuza Yohane, pa Chivumbulutso, kapena pa Chisumbu cha Patmo, “Iwe uyenera kuneneranso pamaso pa mafumu ndi mafuko ndi anthu.” Bukhu la Chivumbulutso likunenerabe. “Iwo amapuma ku zolemetsa zawo, koma ntchito zawo zimawatsatira iwo.” Chikoka chawo chimene iwo anali nacho, chikuwatsatirabe iwo. Mukuona? Ndithudi, izo ziri.

¹⁷⁰ Ndipo tsopano, lero, ife tikupeza chinthu chomwecho, zikoka. Iye uyenera kukopa.

¹⁷¹ Iye tisanayambe kukopa, ife tiyenera kumuzindikira Mulungu, ife tiyenera kukhala oyera, ife tiyenera kukhala odzichepetsa. Iye tiyenera kuzifikitsa tokha pansu, ndi kudziwa, kumangolingalira ndi kumadziwa momwe iwe uliri wamng’ono. Inu sindinu kanthu. Ine sindine kanthu. Ndipo palibe wa ife ali kalikonse, koma Iye zonse. Iye ndi woyenera matamando onse, O Mwanawankhosa wa Mulungu. Chimene ife tikusowa

ndi kubwerera ku kachisi, ife tiyenera kubwerera ku guwa la nsembe la Mulungu ndi kupanga guwa mmitima yathu yomwe, kumene ife tingakhoze kudzipereka tokha, ndiyeno nkumuwona Ambuye Mulungu wa makamu akubwera pansi mmasiku otsiriza ano ndi kuchita zomwe Iye anachita pamene Iye anali kuno poyamba. Ndiye inu mudzamvetsa zimenezo, ndipo mudzafuula, “Watsoka ndi ine!”

Pamene khala la Moto linamukhudza mneneri,
Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro
akanakhalira,

Pamene Liwu la Mulungu linati, “Ndani atipitire ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ambuye, pano, nditumeni ine.”

¹⁷² Ndi kulondola uko? Tiyeni tiyimbe iyo.

Yankhulani, Ambuye wanga, yankhulani,
Ambuye wanga,

Yankhulani, ndipo ndidzafulumira
kuyankha...ine;

Yankhulani, Ambuye wanga, yankhulani,
Ambuye wanga,

Yankhulani, ndipo ine ndidzayankha,
“Ambuye nditumeni ine.”

Mvetserani, abwenzi:

Mamillioni tsopano mu tchimo ndi manyazi
akufa,

Mvetserani ku kulira kwawo kwachisoni ndi
kowawa;

Fulumirani, m'bale, fulumirani
kuwapulumutsa iwo;

Mwamsanga yankhani, “Ambuye, ndine pano.”

Tsopano yankhulani, Ambuye wanga,
yankhulani, Ambuye wanga,

Yankhulani, ndipo ndifulumira kukuyankhani
Inu;

Yankhulani, Ambuye wanga, yankhulani,
Ambuye wanga,

Yankhulani, ndipo ine ndidzayankha,
“Ambuye nditumeni ine.”

¹⁷³ Kodi inu mukumukonda Iye? Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, mphindi yokha, ndipo tizing'ung'uza iyi.

...khala la Moto linamukhudza mneneri,

¹⁷⁴ Tiyeni tiziying'ung'udza iyo tsopano.

Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro
akanakhalira,

Pamene Liwu la Mulungu linati, “Ndani atipitire ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ambuye, pano, nditumeni ine.”

Yankhulani, Ambuye wanga, yankhulani,
Ambuye wanga,
Yankhulani, ndipo ndifulumira kukuyankhani
Inu;

Yankhulani, Ambuye wanga, yankhulani,
Ambuye wanga,
Yankhulani, ndipo ndiyankha, “Ambuye,
nditumeni ine.”

¹⁷⁵ Atate Akumwamba, ife tikuyembekezera kuyeretsedwa kwa kusakhulupirira konse, pakuti moona mamillioni ambiri tsopano mu tchimo ndi manyazi akufa. Ubwino wanji, Ambuye, umene umatero, kuti ife—kuti ife tizidzinenera, kuti tisamadzinenera zimene timaganiza kuti tiri nazo? Izo zimachita ubwino wanji kwa ife kuti tiyesere kulingalira ndi nzeru zathu kuti chinachake chachitika, pamene ife kwenikweni tikudziwa kuti izo sizinachitike? Atate athu Akumwamba, ife tikupemphera kuti Inu mutiyeretse ife tsopano ku kusakhulupirira kwathu konse, ndi zinthu zathu zonse zachithupithupi za moyo, kuti ife tikhoze kukhala oyera mwa Magazi a Ambuye Yesu.

¹⁷⁶ Gulu ili kuno ku Chicago, mwa masomphenya aja mmawa wina, Ambuye, ine ndikudziwa kuti pali gawo la Mkwatibwi ameneyo akuyembekezera apa, ndipo ine sindikudziwa momwe ndingagwirire izo, Ambuye. Ine ndikungofesa mbewu kulikonse komwe ine ndingathe. Ine ndikupemphera, Mulungu, ngati alipo iwo pano, usikuuno, amene—amene amene—amene alibe chowachitikirira ichi, kuti iwo sanayambe akhalapo ndi kuwona Ufumu weniweni wa Mulungu ukuwonetseredwa, sanamvererepo konse zotsatira za zimenezo, ndi kuwona miyoyo yawo ikugwirizana ndi Mawu onse, ndikukhoza, ndi zina zotero; Ambuye, perekani usikuuno kuti uwu ukhale usiku umene iwo ati adzachite zimenezo. Perekani izi, Atate. Ife tikupemphera izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁷⁷ Tsopano molemekeza. Ine—ine ndikutsimikiza inu mumandidziwa ine bwino, kapena ine ndikuyembekezera inu mumatero. Ine sindine wotentheka. Ngati ine ndiri, ine—ine sindikuzidziwa izo. Ndipo ine sindimakhulupirira kuti Mulungu amalemekeza otentheka. Zaka zonsezi, ndi kumunda, pakanakhala chinachake chitachitika. Ine ndine m’bale wanu. Koma ine—ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti. . . Tsopano ine sindinganene kuti Ambuye anandiiza ine, koma ine ndikukhulupirira kuti m’badwo uno umene uli ndi moyo tsopano udzachitira umboni Mkwatulo umenewo. Ndiko kuyandikira kwake, ine ndikukhulupirira. Ine sindingakhoze

kuwona china chirichonse chikubwera. Mwaona, chirichonse chasunthira kumene pa malo ake.

¹⁷⁸ Mukukumbukira chinthu chotsiriza chimene chinachitika Sodomu asanawotchedwe? Ambuye anawonetseredwa mu thupi la munthu. Tsopano, Iye anali Munthu. Iye anadya nyama ndipo Iye anamwa mkaka wa ng'ombe, ndipo anadya mkate wa tirigu, ndipo anadya mwana wa ng'ombe, ndipo anaima pamenepo ndi kudya. Ndipo komabe Abrahamu, amene anayankhula ndi Iye, ananena kuti izo zinali “Mulungu Wamphamvuzonse.” Mu thupi la munthu? Inde. Iye anali kusonyeza chitsanzo cha zimene Iye akanati adzachite mmasiku otsiriza. Yesu analozeranso kwa izo.

¹⁷⁹ Ndipo penyani utumiki umene Iye anauchita. Chinthu choyamba, Iye analozera mmbuyo ku lonjezo Lake. Hmm! Kodi inu mukuyiwona mbali ya fioloje ya izo? Mwaona, Iye anati, “Ine ndinakulonjezani inu, ndipo tsopano Ine ndiri pano kuti ndidzatsimikizire ilo.” Ndipo tsopano momwe ife tikudziwira kuti lonjezo limenelo liri... Penyani izo. Iwo anali kuyembekezera. Motowo usanagwe basi, Abrahamu ndi Sarah anali kuyembekezera mwana wolonjezedwa. Mulungu anawonekera mu thupi la munthu ndipo anachita zizindikiro pamaso pawo, zimenezo Yesu analozerako kuti chidzakhala chinthu chomwecho pa Kudza Kwake, chimene Iye Mwana wolonjezedwa. Ndipo ife tazizindikira izo tsopano kwa, kupitirira, zaka fifitini.

¹⁸⁰ Ndipo komabe mpingo ukuipiraipirabe. Palibe zodabwitsa, ife tikhoza kuwona kuti ife tiri mu M'badwo wa Laodikaya.

¹⁸¹ Tsopano Mzimu Woyera uli pano. Pakhoza kukhala ena mkati muno... Ndife, ndife, ife tiri, ife—ife takhala tikupempherera odwala, koma ine ndikupanga kuyitanira kuguwa. Ine ndikupanga kuitanira ku guwa kwa onse odzinenera ndi iwo amene sanapangapo kudzinenera. Ine ndikukufunsani inu kuti mupite nane ku kachisi wa Mulungu, amene ali mkati mwa inu. Mupite ku kachipinda kovomerezera ka mtima wanu, ndipo mukanene kuti, “Ambuye Mulungu, ndiyeretseni ine. Ndipo mtumizeni Mngelo, ndi khala la Moto, ndipo—ndipo adzachotse kwa ine kusakhulupirira konse, kuti usikuuno ine ndikhoze kuzindikira Kukhalapo kwa Mulungu, monga Yesaya mneneri anachitira pamene Mngelo anamukhudza iye.” Ine ndikufuna inu kuti muchite zimenezo, ndipo mukhaleli woonamtima.

¹⁸² Ndipo tsopano ife tiri nalo lonjezo la m'badwo uno. Ife sitinalonjezedwe gulu lalikulu la zafioloje. Ife tinalonjezedwa...

¹⁸³ Taonani, a—Ahebri anali ndi zaka thuu sauzande za fioloje, koma iwo anali ndi chizindikiro chinaperedwa kwa iwo iwo asanawonongedwe. Loti ndi iwo anali nacho chizindikiro china chinaperekedwa kwa iwo. Iwo anawona chizindikiro

chomwecho. Ndipo tsopano ngati Mulungu awalole anthu... Pamene Yesu anali kuno, Iye anapanga chizindikiro chomwecho kwa Ahebri, Iye anachipanga icho kwa Asamariya, ndipo osati kwa Amitundu.

¹⁸⁴ Tsopano awa ndi mathero a M'badwo wa Amitundu, monga izo zinali pamenepo kwa m'badwo wawo. Mpingo wa Amitundu ukuitanidwa. Tsopano, Mulungu sangakhoze kusintha dongosolo Lake, chifukwa Iye ndi wopandamalire, ndipo Iye ndi wangwiro, wopezeka ponseponse, wodziwa zonse, wamphamvuyonse, ndi wopandamalire. Ngati Iye siali, Iye si Mulungu. Koteri, inu mukuona, Iye ayenera kuti achite chinthu chomwecho chimene Iye anachita nthawi imeneyo. Ndi chifukwa chake iwo ankadziwa mu m'badwo uliwonse kuti Iye amadziwonetsera Yekha, anali mwanjira yomweyo, podziwa kuti Iye ali yemweyo.

¹⁸⁵ Tsopano, ngati Yesu Khristu akanayima pano, usikuuno, pa nsanja iyi, ngati Iye akanayima pano, chinthu chokhacho chimene Iye akanati adzachite, chikanakhala chinthu chomwecho chimene Iye anachita pamene Iye anali kumbuyo kuno, kuti awapangitse anthu kumvetsa kuti Iye anali Mwana wa Mulungu.

¹⁸⁶ Tsopano Iye ali pano. Iye analonjeza kuti adzakhala pano, ndipo tsopano njira yokhayo yomwe Iye angagwirire ntchito ndi pogwiritsa ntchito lonjezo Lake. "Ine ndine Mpesa; inu ndinu nthambi." Ndipo nthambi zimachitira umboni kuti moyo ukuchokera ku mpesa, kapena iwo ulibe moyo uliwonse mwa iwo. Koma ngati iwo wapatsidwa mphamvu ndi moyo, iwo umakhala ndi moyo womwewo umene mpesa uli nawo. Iwo—iwo umadzikakamiza wokha, kapena kudzikankhira wokha mmwamba kupita mu nthambi.

¹⁸⁷ Tsopano khalani molemekeza mphindi. Ndipo mulole Mulungu wa Kumwamba andithandize ine, kuti, inu pa ulaliki uwu umene ine ndaulalikira, kuti pamene... Yesaya, wokhulupirira uja, pamene iye anafika pa malo amene anawona kulephera kwa munthu amene ankayesera kumuimirira Mulungu, ndiye iye anawona Mulungu akutsikira pansi, ndi chenicheni kwa izo, ndiye iye anafuula, "Watsoka ndi ine!" Chifukwa, Mulungu anali atapanga lonjezo monga chomwecho. Iye analipanga ilo kwa m'badwo uliwonse. Iye akulipanga ilo kwa ife, mu m'badwo wathu uwu. Ife tikuwona chirichonse ndendende mu dongosolo la Kubwera Kwake.

¹⁸⁸ Tsopano kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano? Tsopano Iye andithandize ine.

¹⁸⁹ Ndipo ine ndikufuna kuti ndidziwe ndi anthu angati odwala ali kunja uko, kwezani mmwamba manja anu. Inu mukhale ndi chikhulupiro. Ndipo tsopano ine ndikukupemphani inu kuti mutenge Lembu ili, Ahebri, kuti, "Iye ndi Wamkulu

Wansembe wa chivomerezo chathu, ndipo akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu.”

¹⁹⁰ Tsopano inu mupemphere, “Mulungu, ndiroleni ine ndikukhudzeni Inu. Ndiyeno Inu, pondiyankha, muyankhule mobwereza kudzera mwa M'bale Branham, monga Inu munachitira kudzera mwa Mwana Wanu weniweni. Iye ndi mwana wotengedwa kuti aleredwe monga ine. Koma Inu munalonjeza kuti mmasiku otsiriza ano Inu mukanadzachita izo. Tsopano, Ambuye, ndiroleni ine ndiwone chinachake chenicheni.” Ndipo inu muzipemphera.

¹⁹¹ Mulole Mulungu wa Kumwamba, pa maziko a mtima wanga ukutsanuliridwa ku Chicago ndi kulikonse kumene ine ndipite, mulole Iye atsimikizire izo kuti zikhale chomwecho.

¹⁹² Munthu uja yemwe wangodzuka kumene pampando wake, iye ndi munthu wamkulu, wakhala molunjika patsogolo panga apa, yemwe wakweza manja ake mmwamba. Ayi, ali kumbuyoko, wavala malaya oyera. Si kwenikweni inu nokha, koma inu mukupempherera winawake. Ndi mtumiki. Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndikhoza kukuuzani inu chimene chamuvuta iye? Iye ali ndi vuto la mtima. Ngati uko nkulondola, gwedezani dzanja lanu. Mukhulupirire mmalo mwake tsopano.

¹⁹³ Ngati inu mutangokhulupirira! Koma inu muyenera kukhulupirira izo. Ngati inu simukhulupirira izo, izo sizigwira ntchito. Mwamunayo moona mtima.

¹⁹⁴ Apa, apa, apa pakhala mkazi wakhala pansi apa pafupi ndi mapeto awa, mkazi wachiwiri mmbuyo mu mzere wachiwiri apa, pomwe pano. Iye akuvutika ndi matenda a thumbo. Ndi matenda mu thumbo lake. Dona wamng'ono pamapeto apo, wokhala ngati wa imvi, imani pa mapazi anu kuti anthu akhoze kukuwonani inu. Inde, ndi inuyo. Ndicho choonadi. Ndi nthenda mu thumbo, ndiponso inu muli ndi zinthu zina zolakwika, zosokonezeka. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu.

¹⁹⁵ Tsopano kodi iye anakhudza ndani? Osati ine. Iye anamukhudza Iye. Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁹⁶ Apa pali dona wakhala kumbuyo komwe kuno. Iye ali ndi vuto, mmutu mwake mukubangula, wamanjenje, zosokonekera. Akazi a Pfeiffer, inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Imirirani pa mapazi anu. Ine sindikukudziwani inu, koma Yesu Khristu akukupatsani inu chokhumba chanu. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga; iye ndi mlendo kwa ine. Izo zileka. Musadandaule. Chikhulupiro chanu chakuchizani inu.

¹⁹⁷ Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu simukuwona kuti ndicho chimene Iye analonjeza?

¹⁹⁸ Bambo uja wakhala kumbuyo uko. Pamenepo, kodi inu simukuona Kuwala kumeneko? Iye ali moipa kwambiri. Iye

wakhala ali ndi chotupa pakhosi pake. Iye anali ndi opareshoni; dokotala sakumupatsa iye chiyembekezo chochuluka cha icho. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kukhala bwino? Kodi inu mukuvomereza izo, Bambo Stonelake? Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Chabwino, imirirani pa mapazi anu, Yesu Khristu akuchizani inu.

“Ngati inu mungakhulupirire!”

¹⁹⁹ Dona uyu wagana apa pa machira awa. Ndithudi, inu mulibe khadi lapemphero, palibe chinthu choterocho tsopano. Inu mwapuwala. Kodi inu mukukhulupirira izi kuti ndi Choonadi? Kodi inu mukukhulupirira zimene inu mwazimva usikuuno ndi Choonadi? Ngati inu mugone pamenepo, inu mufa. Koma Yesu Khristu akhoza kuchiritsa munthu wakufa ziwalo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye achita zimenezo? Ngati inu muti mukhulupirire izo ndi kuzilandira izo, ndiye inu mukhoza kudzuka pa machira amenewo ndi kumapita kwanu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kuchiritsidwa.

²⁰⁰ Apo iye akubwera, akuwuka kuchokera mmenemo. Winawake amukweze pang’ono apo tsopano, iye ndi wolumala. Winawake... Apo iye akubwera yekha yekha, kuchokera pa mpando, wapangidwa wamphumphu, mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁰¹ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana akusangalala—Mkonzi]. Ndiye imani pa mapazi anu ndipo...

²⁰² Pakubwera mayi wolumala akuyenda kudutsa mwa omvetsera!...?...

Yankhulani, Ambuye wanga... (Dzodzani.)

Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

²⁰³ Pali munthu wina, yemwe anali wopuwala, kuchokera pa kama; anadzuka kuchokera pa machira, akulemekeza Mulungu!

Kodi inu mukukhulupirira?

²⁰⁴ Kodi pali winanso? Machira onse ndi opanda anthu, chirichonse! Aliyense ali pa mapazi ake, akulemekeza Mulungu!

Pamene khala la Moto linamukhudza mneneri!

²⁰⁵ Pali mayi wolumala akuyenda kubwera pa nsanja! Matamando akhale kwa Mulungu! Mpatseni Iye ulemelero ndi matamando!

²⁰⁶ Apa pali bambo wina akubwera pa nsanja. Tayang’anani pa iye akuyenda kukwera masitepe, M’bale Fitch.

²⁰⁷ Tiyeni timupatse Mulungu matamando. Kwezani mmwamba manja anu ndipo mupereke ulemelero kwa Mulungu. 

63-0803^E Chikoka
Lane Tech High School
Chicago, Illinois U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org